# Imani nji!
## Cikhulupiriro ca Atumwi

1. Ndikhulupirira Mulungu
2. Atate wamphamvu wa mphamvu zonse, wakulenga za kumwamba ndi za pansi.
3. Ndikhulupirira Yesu Kristu, Mwana wake wobadwa yekha, Ambuye wathu
4. Amene anapatsidwa ndi Mzimu Woyera, nabadwa mwa Mariya namwaliyo, nasautsidwa kwa Pontio Pilato
5. Namwalira, naikidwa m'manda
6. Natsikira kwa akufa. Tsiku lacitatu anaukanso kwa akufa
7. Nakwera Kumwamba, nakhala padzanja lamanja la Mulungu Atate wa mphamvu zonse, kucokera komweko adzadza kudzaweruza anthu amoyo ndi akufa.
8. Ndikhulupirira Mzimu Woyera. Ndikhulupirira Mpingo wopatulika wa Kristu wa kwa anthu onse
9. Ciyanjano ca oyera mtima, kukhululukidwa kwa macimo,
10. Kuukanso kwa thupi, ndi moyo wosatha. Amen.

## Malangizo a mphunzitsi

- Maphunzirowa ali a anthu onse kuti iwo adziwe ndi kumvetsa mfundo zikulu-zikulu za cikhulupiriro cacikristu monga cafupikitsidwa m'Cikhulupiriro ca Atumwi. M'phunziro mulimonse muli zambiri, ndiye inu monga mphunzitsi, musaye kwambiri ndipo phunzitsani cabe mfundo zikulu-zikulu kotero kuti aphunzi asatayike. Ngati mufuna aphunzi kusalephera kuzindikira mfundozi m'maphunziro, mungalembe Cikhulupiriro ca Atumwi pa pepala lalikulu ndi kulemba mzere pa mbali m'mene muphunzitsa m'phunziro limenelo.
- Colinga ca phunziro <u>lirilonse</u> ciri cimodzi:
  1. Kwa aphunzi akalibe kupulumutsidwa: kumvetsa kuti afunika Yesu kuti iwo alape ndi kukhulupirira Yesu.
  2. Kwa aphunzi opulumutsidwa ndi Yesu: kuwathandiza kukhala okazikika m'uphunzitsi wa Yesu ndi m'mayendedwe ao ndi Mulungu kwa ulemerero wake.
- Osaphunzitsa cabe cidziwitso ca m'Baibulo koma auzeni kuti citanthauzo ca cidziwitsoci ndi cotani m'moyo wa masiku onse.
- M'phunziro lirilonse muli zambiri. Ici cingapangitse aphunzi kulema ndi kusagwira zoonadi zimene muwafuna kudziwa. M'phunziro lirilonse muli sewero kuti aphunzi angapatsidwe mphamvu. Masewero ena mphunzitsi angasankhe ngati aphunzi angawasewere. Ngati aphunzi amacera makutu mungasiye masewero osakakamiza.
- Mphunzitsi asankhe ngati mayeso a m'phunziro lotsiriza adzalembedwa. Ngati mufuna aphunzi kulemba mayeso, muwatengere mayeso monga aliri pa tsamba lotsiriza m'buku iri kapena mulembe mafunso pa bolodi.
- Kuphunzitsa maphunziro awa ndiko udindo waukulu, pakuti pakuphunzitsa muphunzitsa ziphunzitso zikulu kopambana za kupulumutsidwa kwa anthu. Cifukwa cace pamene mukonzekera phunziro, pemphani Mulungu thandizo lake pa kukonzekera phunziro ndi pa kuphunzitsa.

*Munditsogolere m'coonadi canu, ndipo mundiphunzitse; Pakuti ndinu Mulungu wa cipulumutso canga; Inu ndikuyembekezerani tsiku lonseli – Salimo 25.5*

## Phunziro 1 Ndikhulupirira Mulungu

<u>Zofunikira pa nthawi yophunzira</u>
- Baibulo
- Bolodi
- Coko

## 1. Kulandiridwa (10 minutes)
- Landirani onse.
- Fotokozani kuti colinga ca maphunzirowa ndi cakudi anthu adzaphunzira Cikhulupiriro ca Atumwi (afunseni ngati anamva za Cikhulupiriro ca Atumwi ndipo ngati inde, afunseni kuti anamva kuti za Cikhulupiriro ca Atumwi).
- M'phunziro lirilonse tidzawerenga Baibulo pakuti maphunziro onse amangidwa pa zimene Baibulo liphunzitsa. Sitidzaphunzitsa ziphunzitso zobvuta koma zofunikira cabe.

<u>Zidziwitso</u>
- Auzeni kuti maphunziro adzacitika pa tsiku liti ndi pa nthawi yanji. Osacedwa pakuti ngati azicedwa sitidzakhala ndi nthawi yokwanira.
- Ndi cofunikira kwambiri kubwera ku maphunziro onse.
- Aphunzi ayenera kulowa ndi Baibulo m'maphunziro onse. Tidzalifuna pophunzira maphunziro a m'Baibulo.
- M'phunziro lotsiriza tidzalemba mayeso. Kulemba mayeso sikudzakhala bvuto ngati mudzaphunzirako maphunziro onse.

<u>Fotkozani malamulo</u>
- Ana ocepa zaka 18 saloledwa. Osabwera ndi ana ang'ono kapena makanda.
- Osayendayenda pa nthawi ya maphunziro. Pitani ku cimbudzi phunziro lisanayambe.
- Khalani bwino ndipo mverani aphunzitsi. Khalani omasuka pa kukambirana.

- Funsani aphunzi ngati ali ndi mafunso.
- Pemphani Mulungu dalitso pa phunziro iri.

## 2. Kudziwitsidwa kwa mutu wa phunziro (10 minutes)
- Funsani aphunzi ngati akhulupirira.
- Afunseni kuti akhulupirira ciani. Lembani mayankho ao pa bolodi. Funsani mafunso kufufuza zinthu zenizeni zimene akhulupirira. Ngati ayankha 'Mulungu', afunseni kuti ndi ciani cimene akhulupirira zokhudza Mulungu. Ngati ayankha, 'Baibulo', akhulupirira ciani zokhudza Baibulo kodi? Ngati ayankha 'Yesu', ndi ciani cimene akhulupirira cokhudza Yesu kodi?
- Fotokozani kuti tiyenera kudziwa zimene tikhulupirira. Ngati mulemba mayeso ku sukulu, kudziwa mutu cabe sikudzakuthandizani. Muyenera kukhala ndi nzeru za pa mutuwo, cifukwa ngati siciri tero simudzalemba bwino mayeso. Cimodzimodzi kuli Mulungu: sitiyenera kunena cabe kuti tikhulupirira, komanso kudziwa kuti zimene tikhulupirira ndi zotani. Mwa njira ina, izi zonse ziri zopanda mfundo.
- Zonse zimene tiyenera kudziwa zalembedwa m'Baibulo. Zifupikitsidwa m'Cikhulupiriro ca Atumwi. M'phunziro lirilonse tidzaganizirako mbali ina ya Cikhulupiriro ca Atumwi kotero kuti potsiriza maphunziro tidziwa mfundo zikulu-zikulu za m'Baibulo.

## 3. Ndikhulupirira (20 minutes)

- Cikhulupiriro ca Atumwi ciyamba ndi liu 'ndi'. Cikhulupiriro ciri pa munthu. Sitingadalire pa cikhulupiriro ca anthu ena. Uzani aphunzi citsanzo ca banja lakudwala. Aliyense pa yekha ayenera kumwa mankhwala opatsidwa. Ngati mukana cifukwa ena anamwa kale mankhwalawo, mudzafa. Kumwa mankhwala kuli pa munthu. Cikhulupiriro ciri pa munthu.
- Uzani aphunzi kukambirana citanthauzo ca liu 'kukhulupirira'. Kodi kukhulupirira Mulungu ndi kotani?

  Yankho: Kukhulupirira kutanthauza <u>kudziwa coonadi NDIPONSO kuyanjanitsidwa ndi Mulungu</u>.

  1. NZERU: kudziwa ndi kubvomereza Baibulo monga coonadi ca Mulungu. Kutanthauza kukhala otsimikiza kuti Baibulo ndilo coonadi (Yohane 17.17). Tifunika kudziwa Baibulo cifukwa kopanda kuidziwa sitikhoza kukhulupirira!

     Komabe kudziwa cabe si ndiko kufikitsa cikhulupiriro. M'Yakobo 2, Yakobo afotokozera kuti ngakhale ziwanda zikhala ndi cinthu cimene anthu ena amacha cikhulupiriro: ziwanda zidziwa za Mulungu. Koma sizikhala m'ciyanjano ndi Iye (Yakobo 2.19). Ici si cimene Baibulo litanthauza ndi cikhulupiriro. Ndico cakufa kapena cabe (Yakobo 2.20).

     Tingadziwe kuti Mulungu aliko koma ngati tidziwa cabe, kudziwa sikufikitsa cikhulupiriro ca m'Baibulo. Ngati tidziwa cabe za Mulungu koma si ndife oyanjanitsidwa ndi Iye mwa Yesu, timacita cimodzimodzi monga ziwanda zicita.
  2. MTIMA: kukhala oyanjanitsidwa ndi Mulungu. Kutsimikizidwa ndi Mzimu Woyera wa Mulungu kuti Mulungu anakukhululukirani macimo anu mwa Yesu Kristu (Aroma 5.1, Aroma 3.20-26). Ici citanthauza kulapa macimo ndi kudalira pa cipulumutso cake. Kukhulupirira kutanthauza kukhala m'ubwenzi ndi Mulungu mwa Yesu. Kumudziwa ngati Bwenzi.
- Kuli zitsanzo ziwiri zofotokozera za zigawo ziwiri zofunikia pa cikhulupiriro coona:
  - Pamene tadwala, sitithandizika ngati tili ndi mankhwala kunyumba ngati sitikumwa. Cimodzimodzi pa nkhani ya cikhulupiriro: ngati tidziwa za Mulungu koma sitigwiritsa nchito Yesu, Iye satipindulira.
  - Thalauza liri ndi miyendo iwiri. Tifunikira miyendo yonse iwiri kuti lichulidwe thalauza osati nsalu cabe. Cimodzimodzi tiyenera kudziwa za Mulungu/Yesu *komanso* kuyanjanitsidwa naye tisanakambe kuti tikhulupirira.




- Pamene Baibulo likamba za *cikhulupiriro cacing'ono* litanthauza: cikhulupiriro coona (kudziwa ndi ciyanjano/kudalira) koma cikhulupiriroco cisowa mphamvu. Anthu a cikhulupiriro cacing'ono ndiwo okhulupirira oona koma ali ofooka m'cikhulupiriro cao.
- Sitinganene kuti munthu amene adziwa cabe, ndiye munthu wa cikhulupiriro cacing'ono kapena cikhulupiriro cocepa. Monga mwa m'Baibulo, munthuyo alibe cikhulupiriro konse pakuti asowa cinthu cimodzi mwa zinthu ziwiri zofunika kwambiri. Cimodzimodzi monga

thalauza lifunika miyendo iwiri kuti lichulidwe thalauza osati nsalu cabe. Kukhulupirira kutanthauza kudziwa ndi kupezeka m'ciyanjano ndi Mulungu mwa Yesu.

- Acenjezeni kusanena cabe kuti akhulupirira. Kukhulupirira kuli ndi tanthauzo lalikulu. Si kudziwa cabe. Iwo okha amene analandira Yesu akhulupirira moonadi.

## 4. Ndikhulupirira – Kuwerenga Baibulo (20 minutes)

- Werengani pamodzi Marko 9.17-29. Yankhani pamodzi mafunso awa kapena lembani mafunsowa pa bolodi ndipo uzani aphunzi kuwayankha m'magulu ang'ono.

| **Mafunso** |
|---|
| 1. Kodi Mphunzitsi m'ndime ya 17 anali yani? |
| 2. Kodi bvuto la munthu wobwera kwa Yesu linali lotani? |
| 3. Kodi tate anapempha ciani kwa Yesu kulingana ndi ndime ya 24? |
| 4. Nanga ife tiyenera kucita ciani ngati tisowa cikhulupiriro? |
| 5. Cifukwa ciani ophunzira a Yesu sanakhoze kuciritsa mnyamata? |
| 6. Kodi tiona bwanji cikhulupiriro m'nthano iyi? |

- Kambiranani pamodzi mayankho. Mayankho abwino ali conco:
  1. **Kodi Mphunzitsi m'ndime ya 17 anali yani?**
     Yankho: Yesu.

  2. **Kodi bvuto la munthu wobwera kwa Yesu linali lotani?**
     Yankho: Mwana wake anagwiridwa ndi mzimu woipa.
  3. **Kodi tate anapempha ciani kwa Yesu kulingana ndi ndime ya 24?**
     Yankho: Anampempha kuthandiza kusakhulupirira kwake.
  4. **Nanga ife tiyenera kucita ciani ngati tisowa cikhulupiriro?**
     Yankho: Kupempha Yesu kutithandiza, monga mwamunayo anapempha Yesu kuthandiza kusakhulupirira kwake.
  5. **Cifukwa ciani ophunzira a Yesu sanakhoze kuciritsa mnyamata?**
     Yankho: Iwo anayenera kudalira pa Mulungu osati pa iwo okha.
  6. **Kodi tiona bwanji cikhulupiriro m'nthano iyi?**
     Yankho: Yankho: Atate anadziwa (nzeru) kuti ndi Yesu yekha amene akhoza kuthandiza. Anapita kwa Yesu kumpempha thandizo kutanthauza kuti anaika ciyembekezo cake mwa Yesu (ubwenzi).

## 5. Mulungu (15 minutes)

- Uzani aphunzi kukambirana za Mulungu: Kodi Mulungu ndi yani?
- Aloleni kupereka mayankho ao ku gulu lonse.
- Fotokozani kuti kuli zambiri zimene tinganene za Mulungu ndipo zonse zimene tidziwa zopezeka m'Baibulo. Mwacitsanzo:
  - Kuli Mulungu m'modzi wamuyaya (mwacitsanzo Deuteronomo 6.4 ndi Salimo 90.2)
  - Mulungu ali m'modzi mu utatu: Mulungu Atate, Mulungu Mwana ndi Mulungu Mzimu Woyera komabe Mulungu m'modzi (mwacitsanzo 2 Akorinto 13.14, Mateyu 3.17, Mateyu 17.5).
  - Mulungu ndi wacifundo, wacisomo, wolekereza, wa ukoma mtima wocuruka. Asungira anthu osawerengeka cifundo, ali wakukhululukira ndi wolungama ndi woyera (mwacitsanzo Eksodo 34.6 ndi 7).

- Mulungu ndi woyera: wosiyana ndi zina zonse, wopatulika, wokwezedwa kuposa cilengedwe conse, wopanda coipa cina ciriconse, wosadetsedwa ndi wabwino (Eksodo 15.11, Yesaya 57.15, Yobu 34.10, Yesaya 40.25, Yoswa 24.19, Yesaya 6.3-5).

## 6. Sewero (10 minutes)

- Bwerezani kuti kudziwa za m'Baibulo ndi kofunikira. Sewerani sewero kuyesa cidziwitso cao ca m'Baibulo.
- Pangani magulu awiri kapena anai. Funsani gulu limodzi funso limodzi. Ngati adziwa yankho (aloledwa kukambirana monga gulu), iwo apatsidwa pointsi limodzi. Ngati sadziwa yankho gulu lina liyenera kupatsidwa mpata kuyankha.
    1. **Kodi anthu oyamba a pa dziko anali yani?**
       Yankho: Adamu ndi Hava (Genesis 2).
    2. **Chulani dzina la mai wake wa Yesu.**
       Yankho: Mariya (Mateyu 1.16).
    3. **Ndi yani amene anapanga combo?**
       Yankho: Nowa (Genesis 6.13 ndi 14).
    4. **Ndi yani amene anali m'ndende ndipo anasanduka bwana?**
       Yankho: Yosefe (Genesis 39-41).
    5. **Kodi Tabita anali ndi dzina lina lotani?**
       Yankho: Dorika (Macitidwe a Atumwi 9.36).
    6. **Kodi Yakobo anacha bwanji malo momwe iye anapambana ndi Mulungu?**
       Yankho: Penieli (Genesis 32.30).
    7. **Kodi Yesu anatengedwa kapolo m'munda wanji?**
       Yankho: Getsemane (Marko 14).
    8. **Chulani zozizwitsa ziwiri kapena zopambana zimene Yesu anacita.**
       Yankho: Mwacitsanzo kuciritsa wakhate, kucurukitsa mkate ndi nsomba, kuciritsa anthu akhungu.
    9. **Kodi Paulo anachedwa bwanji iye asanasanduke Mkristu?**
       Yankho: Saulo (Macitidwe 9).
    10. **Kodi Yesu anafa m'njira yotani?**
        Yankho: Pa mtanda (Luka 23.33).
    11. **Kodi Yesu anauka patapita masiku angati?**
        Yankho: Masiku atatu (Mateyu 28, 1 Akorinto 15.4).
    12. **Ndi yani amene anaponyedwa m'dzenje napulumuka?**
        Yankho: Danieli (Danieli 6).

## 7. Kutsiriza (5 minutes)

- Bwerezani mwacidule zimene zaphunzitsidwa lero ndipo kambani pamodzi: *Ndikhulupirira Mulungu*.
- Pempherani.

## Phunziro 2 Atate wa mphamvu zonse, wakulenga za kumwamba ndi za pansi

Zofunikira pa nthawi yophunzira
- Baibulo
- Bolodi
- Coko

## 1. Kulandiridwa (5 minutes)
- Landirani onse.
- Pempherani.
- Bwerezani mwacidule zimene zinaphunzitsidwa m'phunziro 1.

## 2. Mulungu Atate – Kuwerenga Baibulo (30 minutes)
- Funsani aphunzi zitsanzo za atate abwino ndi zimene atate awo amacita.
  Yankho: Amakonda ana ao, awasamalira, awaphunzitsa ndi kuwateteza..
- Fotokozani kuti Mulungu Atate ndi Tate wa Yesu. Aliyense amene akhulupirira Yesu ndi wotengedwa m'banja la Mulungu. Mulungu Atate ndi Tate wa Yesu komanso wa ana ake onse obadwa mwatsopano.
- Werengani pamodzi Baibulo kuphunzira zina zambiri za m'mene Mulungu Atate aliri.
  Werengani pamodzi Salimo 68.5 ndipo yankhani funso iri:
  1. **Kodi citanthauza ciani kuti Mulungu ndi Atate wa ana amasiye?**
     Yankho: Asamalira makamaka anthu osatetezedwa (Salimo 146.9, Yeremiya 49.11).

  Werengani pamodzi Salimo 103.13 ndipo yankhani funso iri:
  2. **Funso: Kodi Mulungu Atate acita ciani kulingana ndi ndime iyi?**
     Yankho: Iye ali wacifundo, wosamalira ndi wacisoni kwa ana ake (Yeremiya 31.20, Mateyu 6.32, Yeremiya 31.9).

  Werengani pamodzi Miyambi 3.12 ndipo yankhani funso iri:
  3. **Funso: Cifukwa ciani Mulungu Atate alanga nthawi zina?**
     Yankho: Pakuti afuna kukonzetsa anthu amene alakwa ndipo afuna kuphunzitsa (Ahebri 12.10, Deuteronomo 8.5).
     Ici sicitanthauza kuti mabvuto onse ayambitsidwa ndi macimo athu amunthu (mwacitsanzo Yohane 9.1-3, Yobu 1.8-12, Luka 2.13-14)

  Werengani pamodzi Malaki 1.6 ndipo yankhani funso iri:
  4. **Funso: Kodi Mulungu Atate adandaulira ciani m'ndime iyi?**
     Yankho: Anthu anamucha Mulungu Atate wao, koma sanamlemekeze monga Atate. Ici cinali cizindikiro kuti mitima yao inali kutali ndi Mulungu (Mateyu 15.8).

  Werengani pamodzi Mateyu 6.26 ndipo yankhani funso iri:
  5. **Funso: Kodi Mulungu Atate amacita ciani kulingana ndi ndime iyi?**
     Yankho: Asamalira ndi kulamulira kotero kuti anthu ake sayenera kudera nkhawa pa zocitika (Mateyu 6.25-34).

Werengani pamodzi Yohane 5.26 ndipo yankhani funso iri:

6. **Mafunso: Cifukwa ciani tiyenera kulemekeza Yesu, Mwana wa Mulungu?**
   Yankho: Mwa kucita tero tilemekeza Mulungu Atate (Yohane 15.23, 1 Yohane 2.23, 2 Yohane 1.9).
7. **Ndipo tiyenera kumlemekeza motani?**
   Yankho: Mwa kumkhulupirira Yesu, kumzindikira Iye monga Mpulumutsi wathu ndiponso mwa kudzipereka kwa Iye.

## 3. Wa mphamvu zonse (10 minutes)

- Funsani aphunzi zitsanzo za anthu amene ali ndi mphamvu m'banja, m'mudzi kapena pa dziko.
- Fotokozani kuti Mulungu ali ndi mphamvu kuposa anthu onse ndi zinthu zonse. Mulungu ndi Wamphamvuyonse: akhoza kucita ciriconse cimene afuna. Alamulira zonse, ngakhale pa zinthu zimene ife sitikhoza kulamulira monga Satana ndi imfa.
- Werengerani aphunzi Levitiko 19.31, Levitiko 20.6 ndi Levitiko 20.26-27. Mulungu atiletsa kupita ku mfiti, ng'anga ndi anthu ena amene alankhula ndi mizimu ya anthu akufa. Yesu anagonjetsa Satana (ndi othandiza ake) pamene Iye anafa pa mtanda (Akolose 2.13-15, 1 Yohane 3.18). Anthu a Mulungu aitanidwa kumvera Mulungu yekha ndi kumenyera zoipa mwa mphamvu ya Mulungu (Aefeso 6.11-18).

## 4. Sewero (losakakamiza, 10 minutes)

- Funsani mafunso ena kuphunzitsa aphunzi kuti zonse zimene tiri nazo zacokera kwa Mulungu. Mwacitsanzo mafunso awa:
  - Funsani mphunzi mmodzi ngati adya nsima lero (kapena phala).
  - Funsani wina zimene tifunika kuti tiphike nsima (ufa ndi madzi).
  - Funsani wina kuti ufa ucokera kuti (cimanga).
  - Funsani wina kuchula cinthu cimodzi cimene cimanga cifuna kuti cikule bwino (mvula/dzuwa).
  - Funsani wina kuti mvula ndi dzuwa zicokera kuti (kumwamba).
  - Funsani wina kuti ndi yani kapena ciani cimene cilengetsa dzuwa kuwala ndi mvula kugwa (Mulungu).

  - Funsani mphunzi mmodzi kuti akhala pa ciani (mwacitsanzo mpando)
  - Funsani wina kuti mpando unapangidwa ndi ciani (mtengo)
  - Funsani wina kuti mtengo ufunika ciani kuti ukule bwino (mvula/dzuwa)
  - Funsani wina kuti mvula ndi dzuwa zicokera kuti (kumwamba)
  - Funsani wina kuti ndi yani kapena ciani cimene cipangitsa dzuwa kuwala ndi mvula kugwa (Mulungu)
- Malizitsani ndi kunena kuti Mulungu ndi Mlengi ndi Mwini wa zonse!

## 5. Wakulenga za kumwamba ndi za pansi (20 minutes)

- Fotokozani *mwacidule* kuti m'Baibulo tiwerenga kuti Mulungu analenga zonse (Genesis 1 ndi 2). Analankhula ndipo kunatero. Kusanalengedwe kwa zonse, kunalibe ciriconse koma Mulungu yekha. Analenga kuunika, dzuwa, mwezi, nyenyezi, madzi, mitengo, tizirombo, nyama zikulu-zikulu, Adamu ndi Hava ndi zina zonse zotizungulira. Zonse zinali zabwino, zoyenerera ndi zodabwitsa. Zonse zinakhala m'mgwirizano wabwino: Mulungu, anthu ndi cilengedwe cina.

- Mulungu amasamalirabe cilengedwe cake (Macitidwe 14.17, Macitidwe 17.25). Apangitsa dzuwa kutuluka, mphepho kuomba, ng'ombe kupanga mkaka, mvula kulokwa, matupi athu kugaya cakudya ndi kukhala ndi mphamvu kuti tigwire nchito, ndi zina zotere. Iye ndi Wamphamvuyonse. Ali Atate wabwino. Kulibe cifukwa kuti tingadere nkhawa.
- Adamu ndi Hava, anthu oyamba pa dziko lapansi, anasankha kusamvera Mulungu (Genesis 3). Iyi ndi chimo loyamba. Mulungu akuda chimo. Kuyambira nthawi iyo aliyense ali ndi mtima wocimwa (Yobu 15.14, Miyambi 20.19, Yeremiya 17.19, Aroma 3.23). Ici citanthauza kuti sitikhalabe m'mene Mulungu anafuna ife kukhala. Tili ndi cibadwidwe cofuna kucita zimene sizikondweretsa Mulungu koma cimene cikondweretsa ife eni (Genesis 6.5, Miyambi 7.20, Yesaya 53.6, Yeremiya 18.12). Tilakwa cifukwa tinabadwa ndi mitima yocimwa (Marko 7.21-23, Salimo 51.5).
  Baibulo limagwiritsa nchito mau osiyanasiyana kufotokozera za uchimo wa anthu:
  1. **Akufa** (Aefeso 2.1, Aefeso 2.5, Aroma 5.6). Ngakhale mathupi athu ali amoyo, mizimu yathu iri yosakhoza ndi yosafuna kucita zabwino. Cifukwa cace Baibulo litiuza kuti tibadwe mwatsopano (Yohane 3.3, Yakobo 1.18). Kubadwa mwatsopano kutanthauza kuti mzimu watsopanotu wapangidwa: mzimu/mtima womvera ndi wokondweretsa Mulungu.
     - Monga thupi latsopanotu limapangidwa m'kati mwa mai wake momwemonse umoyo wauzimu ndi cinthu catsopanotu. Kubadwa kwatsopano sikutanthauza *kukonzanso* kwa mzimu wathu koma kutanthauza mzimu *watsopanotu* (Ezekiel 36.26, Yeremiya 24.7)
     - Kuonjezera apa, kubadwa mwatsopano ndiko *mphatso.* Kulibe munthu amene anadzibala yekha. Miyoyo yathu ya thupi ndiyo mphatso. Cimodzimodzinso sitinadzibale tekha m'uzimu. Tinabadwa ndi Mzimu Woyera (Yohane 3.6). Miyoyo yathu yauzimu ndiyo mphatso.

     *Kubadwa mwatsopano kutanthauza kuti cinthu catsopanotu capangidwa. Cifukwa cace zitsanzo zina zonse zilephera. Osagwiritsa nchito zitsanzo zina koma cabe citsanzo ca kubadwa m'thupi cifukwa zitsanzo zina zonze zilephera ndipo anthu angazimvetsa molakwika. M'Yohane 3 Yesu anagwiritsanso nchito citsanzo ca kubadwa m'thupi kuti afotokozere za kubadwa m'uzimu.*

  2. **Udani** (Aroma 5.10, Akolose 1.21). Kulibe ubwenzi pakati pa Mulungu ndi anthu cifukwa ca mitima yathu yocimwa. Uthenga wabwino ndi wakuti Yesu anadza kufa kuti adani a Mulungu ayanjanitsidwe naye.

## 6. Kutsiriza (5 minutes)

- Fotokozani mwacidule zimene zaphunzitsidwa lero ndipo kambani pamodzi: *Ndikhulupirira Mulungu Atate wa mphamvu zonse, wakulenga za kumwamba ndi za pansi.*
- Pempherani.

**Phunziro 3 Ndikhulupirira Yesu Kristu, Mwana wake wobadwa yekha, Ambuye wathu**

<u>Zofunikira pa nthawi yophunzira</u>
- Baibulo
- Coko
- Bolodi

## 1. Kulandiridwa (5 minutes)
- Landirani onse.
- Pempherani.
- Fotokozani mwacidule zimene zinaphunzitsidwa m'phunziro 2.
- M'phunziro lotsiriza tinaphunzira za Mulungu Atate. Lero tidzayamba maphunziro okhudza Mulungu Mwana.

## 2. Ndikhulupirira Yesu (30 minutes)
- Uzani aphunzi kuchula maina a m'masiku onse omwe ali ndi tanthauzo ndipo afunseni cifukwa cace makolo anapatsa mwana wao dzinalo.
- Afunseni citanthauzo ca dzina la Yesu.
- Awerengereni <u>Mateyu 1.21</u> ndipo fotokozani kuti dzina 'Yesu' litanthauza Mpulumutsi.
- Fotokozani kuti Yesu achedwa Mpulumutsi pakuti apulumutsa ku macimo. Akhoza kucotsa chimo ndilo ciyambi ca mabvuto onse. Fotokozani kuti:
  - Cilengedwe cabwino ca Muungu caonongeka cifukwa ca chimo, monga tinaphunzira m'phunziro 2. Ubwenzi wabwino wa Mulungu, anthu ndi cilengedwe cina ziri zoonongeka.
  - Mulungu akuda chimo. Iye ndi wabwino ndi woyera kotero kuti sakhoza kukhala pafupi ndi anthu ocimwa (Yeremiya 59.2, Yesaya 57.7). Anapitikitsa Adamu ndi Hava. Mulungu anakwiya ndi iwo. Iwo anali otayika, anali yekha ndi opanda ciyembekezo.
  - Ifenso monga mbeu ya Adamu ndi Hava ndife otayika, tiri tokha ndi opanda ciyembekezo kopanda Mulungu pakuti tatengera mitima yoipa: ciyambi ca miyoyo yathu ndico cocimwa. Ici citanthauza kuti ndife aucimwa konse: zonse zimene ticita zilephera, ngakhale zabwino zilephera (Yesaya 64.6)!
  - Yesu wosacimwa yekha akhoza kucotsa macimo athu, pakuti Iye anafa pa mtanda (tidzaphunzira zina za imfa yake m'maphunziro otsatira). Ngati Yesu atipulumutsa ku macimo athu, si ndife otayika koma opezeka, osati akufa m'uzimu koma amoyo m'uzimu, osati nekha koma m'banja la Mulungu, osati otembereredwa koma okondedwa ndi Iye, osati olakwa koma oomboledwa.
- Fotokozani kuti cipulumutso ndi codabwitsa. Osacitenga mwa cizolowezi. Lemekezani Mulungu pa mphatsoyo yaikulu yaulere ya cipulumutso imene Mulungu apatsa kwa aliyense amene akhulupirira moonadi (Aefeso 2.8, Aroma 3.24). Ciyambi ca cipulumutso ndico cikondi ca Mulungu ca kwa anthu otayika (nchito zathu zabwino sizitipulumutsa, koma Yesu mwa cisomo) (1 Yohane 4.10, Agalatiya 2.16).
- Yesetsani kufulumizitsa aphunzi kupeza cipulumutso mwa Yesu, pakuti kopanda Yesu ndife otayika ndipo tidzakhala m'Gehena muyayaya. Lapani macimo anu (ici citanthauza kumva cisoni, kuulula macimo ndi kuleka kuwacita) ndipo pemphani Mulungu cikhululukiro. Mulungu afuna kutuma Mzimu wake Woyera kutiphunzitsa kuti tipeze cipulumutso. Afunseni kucita izi!

## 3. Nyimbo (yosakakamiza, 5 minutes)

- Phunzitsani aphunzi nyimbo yogwirizana mutu wa lero. Mwacitsanzo, 'Yang'anani kwa Ine'.

## 4. Kristu (15 minutes)

- Funsani aphunzi zimene zimacitika m'dziko lathu pamene munthu apatsidwa nchito yatsopano ndi yofunikira kwambiri, monga pulezidenti kapena chief.
  Yankho: Aloleni kupereka mayankho okhudza miyambo imene ionetsa kuti munthu apatulidwa kucita nchitoyo.
- Pa nthawi ya m'Baibulo kunali mwambo wa kudzodza anthu amene apatsidwa udindo wapadera (monga mafumu ndi ansembe). Iwo anadzodzedwa ndi mafuta.
- Fotokozani kuti dzina la Kristu m'Cigiriki (cilankhulo ca pa ciyambi ca Cipangano Catsopano) kapena Mesiya m'Cihebri (cilankhulo ca paciyambi ca Cipangano Cakale) litanthauza: wodzodzedwa. Cifukwa cace pamene tinena kuti Yesu ndiye Kristu, titanthauza kuti Yesu ndiye wodzodzedwa (wosankhidwa ndi wokonzekedwa) ndi Atate wake kucita nchito yake yapadera.
- Fotokozani kuti Yesu Kristu anadzodzedwa kukhala:
  1. Mneneri: <u>kuphunzitsa</u> za Mulungu, chimo ndi cipulumutso (Luka 24.19, Yohane 6.14).
  2. Wansembe: <u>kupempherera</u> anthu ake (1 Johane 2.1, Aroma 8.34, Yohane 17.9) ndiponso kufa pa mtanda kukhala <u>nsembe</u> ya macimo (Ahebri 10.10-14, Ahebri 9.28).
  3. Mfumu: <u>kulamulira</u> ndi <u>kuteteza</u> (Luka 1.33, Cibvumbulutso 11.15).

## 5. Mwana wake wobadwa yekha – Kuwerenga Baibulo (20 minutes)

- Werengani pamodzi <u>Yohane 3.14-18</u>. Yankhani pamodzi mafunso awa kapena alembeni pa bolodi ndipo uzani aphunzi kuwayankha m'magulu ang'ono.

**Mafunso**
1. Werenganinso ndime ya 14. Kodi Mwana wa munthu amene anayenera kufa pa mtanda ndiye yani?
2. Kodi tiyenera kukhulupirira yani kuti tipulumuke?
3. Kodi Mulungu anatuma yani ku dziko lapansi, kulingana ndi ndime ya 16?
4. Werenganinso ndime ya 17. Cifukwa ciani Mulungu anatuma Mwana wake?
5. Nanga inu, mungapatse mwana wanu kupulumutsa adani anu?

- Kambiranani pamodzi mayankho. Mayankho abwino ali conco:
  1. **Werenganinso ndime ya 14. Kodi Mwana wa munthu amene anayenera kufa pa mtanda ndiye yani?**
     Yankho: Yesu Kristu.
  2. **Kodi tiyenera kukhulupirira yani kuti tipulumuke?**
     Yankho: Yesu Kristu, Mwana wa munthu.
  3. **Kodi Mulungu anatuma yani ku dziko lapansi, kulingana ndi ndime ya 16?**
     Yankho: Mwana wake wobadwa yekha, Yesu Kristu.
  4. **Werenganinso ndime ya 17. Cifukwa ciani Mulungu anatuma Mwana wake?**
     Yankho: Kupulumutsa aliyense amene amkhulupirira.
  5. **Nanga inu, mungapatse mwana wanu kupulumutsa adani anu?**
     Yankho: Aliyense ayankhe pa yekha.

- Malizitsani ndi kunena kuti Yesu ndi Mwana wa Mulungu wobadwa yekha (Yohane 1.18, 1 Yohane 4.9). Ana ena onse a Mulungu atengedwa m'banja la Mulungu (Aefeso 1.5-6).

## 6. Ambuye wathu – zolowapo (15 minutes)

- Mbuye ndiye mwini wa cinthu. Ganizirani munthu amene ali ndi malo obwereketsa: munthuyo ndiye mwini wa malo.
- Pamene tinena kuti tikhulupirira Yesu Kristu monga Ambuye wathu tiulula kuti Iye anatifera ndiponso kuti ndife ake (Akolose 1.13-14, 1 Petro 1.18-19). Sitiri a ife eni kapena a Satana koma a Yesu ndipo tifuna kulondola cifuniro cace m'miyoyo yathu (1 Akorinto 6.20).
- Werengerani aphunzi colowapo ici ndipo auzeni kukambirana m'magulu ang'ono zimene Lameck ndi Leya ayenera kucita.
  *Lameck ndi Leya ali ndi ana anai. Iwo ndiwo banja lacikristu ndipo afuna kumvera Mulungu yekha. Tsiku lina mwana wao wakhanda adwala kwambiri. Iwo aopa kuti mwana adzamwalira. Anthu ena akamba kuti mwana adwala cifukwa ca kusabvala thumwa imene ingatetezere mwana kuli mizimu yoipa.*
  Yankho: Ayenera kukhala oima nji ndi osakayika: Yesu ali ndi mphamvu zonse ndipo aliyense amene ali ake ali otetezeka. Satana angagwiritse nchito zocitika kusokoneza Lameck ndi Leya koma iwo ayenera kupitiriza kudalira pa Mpulumutsi wao Yesu Kristu, kupita ku cipatala ndi kupempha Mulungu kuonetsa mphamvu yake mwa kuciritsa mwana wao.
- Werengerani aphunzi colowapo ici ndipo auzeni kukambirana m'magulu ang'ono zimene Samson ndi Misozi ayenera kucita.
  *Samson ndi Misozi anayamba ukwati wao zaka zitatu zitapitazo. Mosachedwa Misozi anayamba kudandaula cifukwa ca Samson. Anauza anzake, 'Sindikondwera cifukwa ca makhalidwe a mwamuna wanga. Akamba kuti kulibe munthu amene angamuuze kucita ciani. M'malo mwa kusamalira banja, iye aononga nthawi ndi ndalama. Sathandiza banja kukhala bwino. Ku calichi iye akamba kuti ndiye Mkristu ndipo anthu akonda kumumvera kulalikira mwamphamvu. Iwo sadzandikhulupirira'.*
  Yankho: Munthu amene akamba kuti iye ndiye Mkristu saloledwa kucita ciriconse cimene afuna, koma ayenera kumvera Yesu Mbuye. Yesu ndi Mbuye wake. Cifukwa cace munthuyo ayenera kukhala monga mwa cifuniro ca Mulungu cimene cilembedwa m'Baibulo. Izi zikhudza zonse m'miyoyo yathu: ndalama, nthawi, banja, matupi athu ndi zina zotere. Samson ayenera kutsutsidwa kuti alape (kumva cisoni, kuulula, kuleka) macimo ake. Misozi ayenera kuima nji ndi kupempha anthu kumthandiza.

## 7. Kutsiriza (5 minutes)

- Fotokozani mwacidule zimene zaphunzitsidwa lero ndipo kambani pamodzi: *Ndikhulupirira Mulungu Atate wamphamvu wa mphamvu zonse, wakulenga za kumwamba ndi za pansi. Ndikhulupirira Yesu Kristu, Mwana wake wobadwa yekha, Ambuye wathu.*
- Pempherani.

## Phunziro 4 Amene anapatsidwa ndi Mzimu Woyera, nabadwa mwa Mariya namwaliyo, nasautsidwa kwa Pontio Pilato

<u>Zofunikira pa nthawi yophunzira</u>
- Baibulo
- Bolodi
- Coko

### 1. Kulandiridwa (5 minutes)
- Landirani anthu onse.
- Pempherani.
- Fupikitsani zimene zinaphunzitsidwa m’phunziro 3.
- Tinaphunzira kuti Yesu Kristu ndiye Mpulumutsi wotumidwa ndi Mulungu. M’phunziro la lero ndi m’maphunziro otsatira tidzaphunzira zimene Yesu anacita kupulumutsa anthu ocimwa.

### 2. Amene anapatsidwa ndi Mzimu Woyera – Kuwerenga Baibulo (30 minutes)
- Fotokozani kuti tinaphunzira kuti Yesu ndi Mulungu. Koma anakhalanso munthu. Ici ndi cinthu codabwitsa.
- Werengani pamodzi <u>Luka 1.26-38</u> ndipo yankhani mafunso awa kapena alembeni pa bolodi ndipo uzani aphunzi kukhala m’magulu kuyankha mafunsowa.

**Mafunso**
1. Fotokozani mwacidule zimene zinacitika m’nthano.
2. Kodi ndi yani amene anatuma mngelo kwa Mariya?
3. Cifukwa ciani mngelo anati kuti Mariya anapeza cisomo ndi Mulungu?
4. Kodi Yesu ali Mwana wa yani, kulingana ndi ndime ya 32?
5. Mariya anadabwa cifukwa ca mau a mngelo: iye sanakwatiwe, ndiye angakhale bwanji ndi Mwana? Kodi mngelo anamuyankha ciani?
6. Werenganinso ndime ya 35 ndipo fotokozani cifukwa ciani Yesu alibe macimo, ngakhale Iye anakhala Munthu.

- Mayankho abwino ali conco:
  1. **Fotokozani mwacidule zimene zinacitika m’nthano.**
     Yankho: Mngelo anauza Mariya kuti adzabala Mwana, Ambuye Yesu Kristu.
  2. **Kodi ndi yani amene anatuma mngelo kwa Mariya?**
     Yankho: Mulungu.
  3. **Cifukwa ciani mngelo anati kuti Mariya anapeza cisomo ndi Mulungu?**
     Yankho: Pakuti adzakhala ndi Mwana: Yesu, Mwana wa Mulungu.
  4. **Kodi Yesu ali Mwana wa yani, kulingana ndi ndime ya 32?**
     Yankho: Mwana wa Wamkulukulu, Mwana wa Mulungu.
  5. **Mariya anadabwa cifukwa ca mau a mngelo: iye sanakwatiwe, ndiye angakhale bwanji ndi Mwana? Kodi mngelo anamuyankha ciani?**
     Yankho: Mzimu Woyera adzapanga thupi la Yesu kuti abadwe pa dziko lapansi.
  6. **Werenganinso ndime ya 35 ndipo fotokozani cifukwa ciani Yesu alibe macimo, ngakhale Iye anakhala Munthu.**
     Yankho: Iye ali woyera, pakuti Mulungu ndi Atate wake. Iye ndiye Mulungu komanso Munthu: Munthu wosalakwa.

- Fotokozani kuti Yesu ndi Mulungu konse (1 Yohane 5.20, Akolose 1.15-14) ndiponso munthu konse (Yohane 1.14, Agalatiya 4.4, Afilipi 2.7). Mpulumutsi anayenera kukhala Mulungu komanso munthu:
  - **Munthu.** Adamu, woimirira umunthu wonse, anacimwa. Cifukwa cace umunthu anayenera kunyamula cilango ca Mulungu ca pa uchimo (Levitiko 5.17, Agalatiya 3.10, Aroma 2.6). Yesu anasanduka munthu. Sanacimwe (1 Petro 2.22). Sanayenere kunyamula macimo ake ndi cilango ca Iye mwini. Cifukwa cace anakwaniritsa kuimirira anthu amene anacimwa (2 Akorinto 5.21, Ahebri 7.26-27, Ahebri 2.14, Ahebri 2.17).
  - **Mulungu**. Kulibe munthu amene akwaniritsa kunyamula mkwiyo wa Mulungu wa pa macimo. Mkwiyo wa Mulungu ndi woopsya (Deuteronomo 4.24, Nahumu 1.6) ndipo kulibe amene akwaniritsa kuunyamula koma Mulungu yekha. Yesu ndi Mulungu ndipo cifukwa cace Iye anakwaniritsa kunyamula mkwiyo wa Mulungu ndi kugonjetsa macimo ndi imfa.

  Yesu yekha ndiye Mkhalapakati pakuti Iye ndiye Mulungu komanso Munthu (1 Petro 3.18).
- Yesu adziwa zobvuta za m'moyo (Ahebri 4.15, Ahebri 2.8) ndipo akhudzidwa ndi zofooka zathu.

## 3. Nabadwa mwa Mariya namwaliyo (20 minutes)

- Uzani aphunzi kukhala m'magulu ang'ono kuuzana zimene adziwa za kubadwa kwa Yesu. Itakomana 10 minutes, auzeni kupereka mayankho ao kwa gulu lonse. Pangani nthano yabwino ya zimene zinacitika mogwiritsa nchito mayankho ao. Dziwitseni kuti akamba za: Yosefe ndi Mariya, Betelehemu, nyumba ya alendo, khola, nsalu, angelo, nyimbo ya angelo, azibusa, Simeoni ndi Anna m'Kacisi ndiponso za amuna anzeru a ku m'mawa. Ngati alephera kuyankha, auzeni mwacidule nthano monga ilembedwa m'Luka 2 ndi Mateyu 2.
- Yesu anadzicepetsa pa kubadwa pa dziko lapansi (Afilipi 2.7-8, Yohane 1.10, Ahebri 12.2, Mateyu 8.20). Mfumu wa kumwamba ndi wa dziko lonse lapansi anasanduka mwana wakhanda, wosauka ndi wopanda mphamvu, wokhala m'khola. Anacita tero kuti apereke ana ake osauka ndi opanda mphamvu ku Mwamba (2 Akorinto 8.9)! Caka ciriconse pa tsiku la Krisimasi timakumbukira codabwitso ici ca Mulungu.
- Funsani aphunzi zimene Yesu anacita pamene anakula.

  Yankho: Anacitira anthu onse zabwino, makamaka mwa kuciritsa anthu. Anaphunzitsa anthu za Ufumu wa Mulungu. Anawauza kulapa ndi kumkhulupirira. Anawacenjeza kusakhala okhutidwa ndi iwo mwini kapena ndi cipembedzo koma kupeza mtendere ndi Mulungu mwa Yesu.
- Yesu anadza kuononga nchito ya Satana (1 Yohane 3.8). Yesu anadza kugonjetsa chimo ndi imfa kotero kuti Ufumu wa Mulungu umangidwe ndi kukonzedwanso (Mateyu 4.17, Akolose 1.13).

## 4. Sewero (losakakamiza, 10 minutes)

- Lembani pa bolodi:

| | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|
| M | A | R | I | Y | A | U |
| U | S | E | Y | S | A | S |
| L | Z | O | N | S | E | A |
| U | M | Z | I | M | U | O |
| N | I | T | A | K | A | P |
| G | L | L | S | C | P | E |
| U | C | I | S | O | M | O |

- Uzani aphunzi kupeza mau awa:
  Mariya Yesu Mulungu cisomo
  zonse pakati usaope Mzimu

## 5. Nasautsidwa kwa Pontio Pilato (20 minutes)

- Uzani aphunzi kuti Satana ndi anthu anada Yesu m'mene Iye analiri ndi pa zimene anacita pa dziko lapansi. Yesu anazondedwa ndi:
  - **Satana**.
    Satana sanafune Yesu kuphunzitsa anthu za Mulungu ndi kukhala Mpulumutsi (Luka 22.3, Marko 1.13)
  - **Anthu**.
    - Anthu ambiri sanakhulupirire kuti Yesu ndi Mwana wa Mulungu (Marko 3.22, Yohane 10.20, Yohane 8.48-49, Luka 7.39). Anayembekezera Mesiya (Kristu) amene adzawapulumutsa ku adani ao a pa dziko lapansi (Yohane 7.19, Macitidwe 1.6, Mateyu 20.21, Yohane 18.36).
    - Ambiri anazonda Yesu pa kukonda anthu ocimwa (Luka 5.30, Luka 19.7). Anaganiza kuti munthu wopembedza ayenera kuzonda anthu ocimwa.
    - Ambiri anazonda Yesu pa kuphunzitsa kwake kwa kulapa ndi cikhulupiriro mwa Iye. Anakhulupirira kuti kusunga malamulo a Mulungu adzawapangitsa kukhala obvomerezeka pa maso pa Mulungu. Anasunga malamulo a Mulungu molongosoka ndipo anayembekeza kuti Mulungu adzawalandira cifukwa ca makhalidwe ao abwino koma sanamvetse kuti mitima yao inali patali ndi Mulungu (Luka 11.39, Yohane 9.40-41, Mateyu 15.1-20). Yesu anawaphunzitsa kuti Iye yekha akwaniritsa kuyanjanitsa anthu ndi Mulungu (Yohane 14.6). Sitipulumutsidwa ndi zocita zathu koma ndi cikhulupiriro mwa Yesu (Aroma 3.28). Yesu anaphunzitsa kuti kulapa ndi kofunikira. Iwo okha amene alapa ndi kukhulupirira Yesu adzalandiridwa ndi Mulungu (Mateyu 21.32).
- Fotokozani *mwacidule* zimene zinacitika ndi Yesu kulingana ndi Mateyu 26.14-75 ndi Mateyu 27.1-32.
- Fotokozani kuti m'zowawa zake Yesu anakhalabe Mulungu. Anali ndi mphamvu kuposa adani ake. Koma sanawaletse: anafuna kukhetsa mwazi wake ndi kufera ana ake obvutika ndi akufa m'uzimu. Ico cinali colinga cace. Cikondi cacikulu ndithu!

## 6. Kutsiriza (5 minutes)

- Fotokozani mwacidule zimene zaphunzitsidwa lero ndipo kambani pamodzi: *Ndikhulupirira Mulungu Atate wamphamvu wa mphamvu zonse, wakulenga za kumwamba ndi za pansi. Ndikhulupirira Yesu Kristu, Mwana wake wobadwa yekha, Ambuye wathu amene anapatsidwa ndi Mzimu Woyera, nabadwa mwa Mariya namwaliyo, nasautsidwa kwa Pontio Pilato.*
- Pempherani.

**Phunziro 5 Namwalira, naikidwa m'manda**

Zofunikira pa nthawi yophunzira
- Baibulo
- Bolodi
- Coko

## 1. Kulandiridwa (5 minutes)
- Landirani anthu onse.
- Pempherani.
- Fotokozani mwacidule zimene zinaphunzitsidwa m'phunziro 4.

## 2. Namwalira (15 minutes)
- Funsani aphunzi kuti kupacikidwa ndi kotani.
  Yankho: Kukhoma munthu pa mtanda ndi colinga kuti munthuyo afe. Masiku a kale anapacika anthu oipa koposa cabe. Baibulo sikamba zambiri za kupacikidwa pa mtanda kupatula imfa ya Yesu. Komabe m'Cipangano Cakale tiwerenga ndime zina za anthu amene anapacikidwa pa mtengo kapena mtanda iwo angakhale anali amoyo kapena akufa (Deuteronomo 21.22-23, Yoswa 10.26)
- Fotokozani zimene zinacitika pamene Yesu anali pa mtanda kulingana ndi Mateyu 27.33-49.
- Werengerani aphunzi Agalatiya 3.13 ndipo afunseni citanthauzo ca ndime iyi ya m'Baibulo.
  Yankho: Ife ocimwa ndife otembereredwa ndi Mulungu pakuti tilephera kumumvera moyenera. Kulibe ciriconse cimene tingacite kucotsa temberero la Mulungu la pa miyoyo yathu. Koma Yesu yemwe anakhala temberero mwa kuimirira m'malo mwa anthu otembereredwa amene alapa (kumva cisoni, kuulula, kuleka) ndi kudalira pa cipulumutso cace (kugonja ndi kumlandira). Yesu anakhala temberero kudalitsa anthu ake!

## 3. Namwalira – Kuwerenga Baibulo (30 minutes)
- Werengani pamodzi Yohane 19.30 ndi Mateyu 27.50-56.
- Yankhani pamodzi mafunso awa:
  1. **Yesu anati 'Kwatha', Iye asanafe. Ndi ciani cimene cinatha?**
     Yankho: Nchito yake ya pa dziko lapansi, kuzunzidwa kwake, nchito ya kuombola.
  2. **Kodi citanthauza ciani kuti Yesu anatha zonse?**
     Yankho: Citanthauza kuti tsono kuli njira yopita Kumwamba. Iye anacita zonse zofunikira. Sitiyenera kuonjezapo, koma kulandira cipulumutso mwa cisomo.
  3. **Kodi citanthauza ciani kuti Yesu anapereka mzimu?**
     Yankho: Anafa. Zindikirani umoyo wake sunatengedwe kwa Iye koma kuti *anapereka* moyo wake. Anali wolamulira nthawi zonse.
  4. **Ndi ciani cimene cinacitika pa nthawi ya imfa ya Yesu?**
     Yankho: Cinsaru cocinga ca m'Kacisi cinang'ambika pakati kucokera kumwamba kufikira pansi, dziko linagwedezeka ndipo anthu ambiri akufa anauka. Citanthauzo ca zizinkikiro izo (*fotokozani mwacidule)*
     - Cinsaru cocinga ca m'Kacisi cinang'ambika. Cinsaru cocinga ca m'Kacisi cinali katani limene linagawira zipinda ziwiri: malo opatulika ndi malo opatulikitsa (kumene Mulungu anakhala masiku a kale) (Eksodo 26.33). Kunalibe munthu amene analoledwa kulowa malo opatulikitsa komabe wamkulu wansembe

kamodzi pa caka. Cinsalu cinasonyeza kuti Mulungu ndi anthu ndiwo olekanitsidwa cifukwa ca macimo. Pamene Yesu anafa, Iye anacotsa macimo a anthu ake ndipo anthu ace tsono akhoza kukhala pafupi ndi Mulungu cifukwa ca Iye. Cifukwa ca Yesu tiloledwa kupita kwa Mulungu mwa pemphero molimbikia mtima. Tiwerenga za citanthauzo ca cinsalu cong'ambika m'Ahebri 9 ndi 10. Ngati mufuna, awerengereni aphunzi Ahebri 9.2-12 kuti amvetsetse zina izi. Zindikirani kuti Baibulo litiuza kuti cinsalu cinang'ambidwa kucokera kumwamba kufikira pansi. Ndi Mulungu amene anang'amba cinsalu kuonetsa kuti anthu ocimwa aloledwadi kukhala pafupi naye mwa Yesu.

   - <u>Dziko linagwedezeka</u>. Zivomezi zinacitika kawirikawiri m'Israyeli. Nthawi zina zivomezizo zinaphunzitsa anthu cina cace, mwacitsanzo mphamvu ya Mulungu ndi kupezekamo kwake (Salimo 68.7-8, Eksodo 19.18, 1 Samueli 14.15) ndi mkwiyo wa Mulungu wa pa macimo (Yesaya 5.25, Nahumu 1.5-6, 1 Samueli 14.15). Pamene Yesu anafa, mphamvu ya Mulungu, kupezekamo kwake ndi mkwiyo wake zinaoneka m'civomezi cimene cinali camphamvu kotero kuti miyala inang'ambika.
   - <u>Anthu akufa anauka kwa akufa</u>. Yesu anagonja macimo ndi imfa mwa imfa yake. Iye ndiye Wopambana. Anthu ake ali ndi moyo wosatha cifukwa ca imfa yake (Aroma 5.10). Baibulo sitiuza zambiri za anthu awa. Tidziwa cabe kuti anaonekera kwa anthu ambiri kukhala mboni za imfa ya Yesu ndi kuuka kwake.

5. **Kodi mkulu wa asirikali anati ciani?**
   Yankho: Indedi Uyo ndiye Mwana wa Mulungu
6. **Kodi ndinu otsimikiza kuti Yesu ndi Mwana wa Mulungu?**
   Yankho: Aliyense ayankhe pa yekha.

- Phunzitsani aphunzi cofunikira ca imfa ya Yesu.
  - <u>Yesu ayanjanitsa adani ndi anthu osapembedza ndi Mulungu</u> (Akolose 1.21-23, Aroma 5.6). Cifukwa ca macimo athu ndife adani a Mulungu ndi akufa m'uzimu. Mwa imfa ya pa mtanda Yesu anacotsa macimo. Cifukwa ca Iye anthu akhoza kuyeretsedwa ku macimo ao ndi kuyanjanitsidwa ndi Mulungu mwa cikhulupiriro ca mwa Yesu. Yesu ayanjanitsidwa adani ndi Mulungu!
  - <u>Yesu asinthanitsa macimo ndi cilungamo cace</u> (2 Akorinto 5.21, Tito 3.3-7, Agalatiya 3.10-13). Yesu ali wosacimwa. Ananyamula macimo ndi temberero za anthu ake kuti iwo akhale olungama ndi opanda pace pa maso pa Mulungu. Yesu amacita tero mwa cisomo ndi cikondi, osati cifukwa tinacita cina cake comkondweretsa Iye. Ndi mphatso.
  - <u>Yesu anagonjetsa macimo ndi Satana</u> (Ahebri 2.14-15). Anthu ake sayenera kukhalabe ndi mantha ndi mwa ukapolo.
- Uzani aphunzi kuti timakumbukira imfa ya Yesu caka ciriconse pa tsiku Lacisanu Loyera. Kodi tsiku Lacisanu Loyera ndi tsiku labwino kapena loipa?
- Fulumizitsani aphunzi kupeza umoyo wauzimu mwa imfa ya Yesu. Iye ndiye cifukwa cakuti tikhoza kuyanjanitsidwa ndi Mulungu m'malo mwa kukhala kutali ndi Mulungu muyayaya. Kumbukirani kuti Yesu ayanjanitsa anthu ocimwa (adani) ndi Mulungu. Ici citanthauza kuti sitifunika kukhala anthu opanda chimo tisanakhoze kulandiridwa ndi Yesu. Ngakhale ngati sitikumva cisoni pa macimo athu, tifunika kupita kwa Yesu pakuti Iye yekha mwa Mzimu wake Woyera atiphunzitsa zimene tifunika kudziwa.
- Akumbutseni citsanzo ca mankhwala: tikadwala tiyenera kumwa mankhwala pakuti mwa njira ina mankhwalawo satipindulira. Tiyenera kugwiritsa nchito Yesu pakuti mwa njira ina imfa yake sitipindulira!

## 4. Namwalira – Aroma 6.6 ndi 1 Petro 2.24 – zolowapo (20 minutes)

- Awerengereni aphunzi Aroma 6.6 ndi 1 Petro 2.24.
- Fotokozani citanthauzo ca ndime izi.
  Aliyense amene akhulupirira Yesu anafa m'uzimu pamodzi ndi Iye. Ici citanthauza kuti iwo saitanidwa kudzitumikira koma kutumikira Mulungu mwa Yesu. Yesu anafa kuwapatsa umoyo wauzimu. Akristu aitanidwa kutumikira Mulungu osati macimo ndi zilakolako zocimwa.
- Kambiranani zolowapo izi.
  *Esneli ali ndi zaka 23. Sali wokwatiwa, koma anagona ndi anyamata osiyanasiyana. Ali ndi ana awiri: Elijah wa zaka 4 ndi Daniel wa caka 1. Esneli abvutika kudyetsa ana ake. Tsiku lina apeza nchito. Esneli auzidwa kuti ngati afuna kugwira nchito imeneyo, iye ayenera kugwira nchito pa tsiku la Sabata ndipo sadzakhoza kupita ku calichi. Esneli abvomereza. Ku calichi lake iye akamba kuti sadzabweranso pakuti adzayamba kupemphera ku calichi lina.*
    1. **Kodi Esneli anatumikira uchimo m'njira yanji?**
       Yankho: Anagona ndi amuna kunja kwa ukwati, anapita ku nchito m'malo mwa ku calichi ndipo ananena bodza. Paulo analemba kuti Akristu ayenera kudziletsa macimo awa (Agalatiya 3.5 ndi 9). Baibulo litiuza kudziletsa macimo awa.
    2. **Kodi iye anayenera kucita ciani m'malo mwa kutumikira chimo?**
       Yankho: Aroma 6.10-14. Ayenera kukhala monga Kristu. Ici citanthauza kukhala moyo monga Yesu anakhala. Yesu anamvera Mulungu nthawi zonse. Mulungu anali wofunikira koposa kwa Iye. Esneli anayenera kukhala ndi moyo woyera, kudziletsa macimo, kupempha anthu ena kumthandiza ndipo cofunikira koposa ndi kuti anayenera kupempha Mulungu kumthandiza kukhala moyo wake monga Mulungu afuna.

  *Chisulo ali ndi zaka 30. Ali wokwatira ndi Victoria. Iwo alibe ana. Chisulo akalipira Victoria. Chisulo aganiza kuti iwo alibe mwana cifukwa ca Victoria. Usiku uliwonse Chisulo akakamiza Victoria kugona naye ndipo akamba kuti, 'Ndinakwatira munthu wosayenera. Ngati simudzandibalira mwana, ndidzakusiyani ndipo wina adzandibalira mwana'. Masiku onse Chisulo amamwa mowa kwambiri kuti aiwale bvuto lake. Ngati alibe ndalama kugula mowa, iye amaba.*
    1. **Kodi Chisulo anatumikira uchimo m'njira yotani?**
       Yankho: Anakhala m'macimo olembedwa m'Marko 7.21-23: maganizo oipa, cigololo (kuganizirako cabe ndi chimo), diso loipa, kuba ndi kupusa. Komanso iye analedzera (1 Akorinto 5.11). Anayendetsedwa ndi zifuniro zake.
    2. **Kodi anayenera kucita ciani m'malo mwa kutumikira uchimo?**
       Yankho: Aroma 6.10-14. Ayenera kukhala monga Kristu., kumene kutanthauza kukhala moyo monga Yesu anakhala. Yesu akonda ndipo anakhala moyo monga mwa cifuniro ca Mulungu. Chisolo anayenera kusamalira mkazi wake mwa cikondi, anayenera kupemphera pamodzi kuti alandire mwana, kusaopseza mkazi wake kumusiya, kusaledzera ndi kusaba.

- Mangirirani ndi kunena kuti Yesu anafa kulipira macimo. Cifukwa cace ife monga anthu ake taitanidwa kudziletsa macimo ndi kukhala miyoyo yathu momvera Mulungu. Mphamvu imene itipangitsa kukhala momvera Mulungu icokera kwa Yesu (Tito 2.14). Tifunika Yesu kutiyeretsa kotero kuti ndife okhala cheru kucita zimene zili bwino kulingana ndi Mulungu.

## 5. Naikidwa m'manda (15 minutes)

- Fotokozani *mwacidule* nthano ya kuikidwa m'manda kwa Yesu monga ilembedwa m'Mateyu 27.57-66.
- Fotokozani citanthauzo ca kuikidwa m'manda kwa Yesu:
  - Yesu anafadi. Ananyamula macimo a anthu ake ndipo macimo ao anaikidwa m'manda pamodzi ndi Iye. Cinthu coikidwa m'manda cacotsedwa konse ndipo ciribe mphamvu. Anthu a Mulungu amasulidwa ku mphamvu ya chimo: mphamvuyo sidzawatenga ku cionongeko m'Gehena.
  - Anthu a Mulungu sayenera kuopa manda. Manda ndi monga cogonapo kumene matupi ao apumula mpaka adzaukidwa ndi kukhala ndi Mulungu muyaya.

## 6. Kutsiriza (5 minutes)

- Fotokozani mwacidule zimene zaphunzitsidwa pamodzi ndipo kambani pamodzi: *Ndikhulupirira Mulungu Atate wamphamvu wa mphamvu zonse, wakulenga za kumwamba ndi za pansi. Ndikhulupirira Yesu Kristu, Mwana wake wobadwa yekha, Ambuye wathu amene anapatsidwa ndi Mzimu Woyera, nabadwa mwa Mariya namwaliyo, nasautsidwa kwa Pontio Pilato, namwalira, naikidwa m'manda.*
- Pempherani.

**Phunziro 6 Natsikira kwa akufa. Tsiku lacitatu anaukanso kwa akufa.**

Zofunikira pa nthawi yophunzitsa
- Baibulo
- Bolodi
- Coko

## 1. Kulandiridwa
- Landirani onse.
- Pempherani.
- Fotokozani mwacidule zimene zinaphunzitsidwa m'phunziro 5.

## 2. Natsikira kwa akufa (15 minutes)
*Kuli maganizo osiyanasiyana kuli mbali iyi ya Cikhulupiriro ca Atumwi. Cilankhulo coyamba ca cikhulupiriroci ca atumwi cikamba, 'hade'. Ici cifanizira manda komanso Gehena. Cifukwa cace mbali iyi ya Cikhulupiriro ca Atumwi ingatanthauze zinthu izi ziwiri:*
1. *Thupi la Yesu linali m'manda pamene mzimu wake unali m'manja a Atate wake.*
2. *Yesu anazunzika zipsinjo za m'Gehena. Anamva konse mkwiyo wa Mulungu wa kwa chimo. Cipsinjo ici cinali cozama kwambiri ndipo cifukwa cace ici cipezeka potsiriza pa mbali iyi ya Cikhulupiriro ca Atumwi.*

- Funsani aphunzi za maganizo ao okhuza Gehena: Gehena uoneka bwanji, ndani aliko ndi zina zotere.
  Yankho: Gehena ndi malo oipa koposa. Ndipo ndi wamuyaya. Ndi malo omwe Satana akhala pamodzi ndi iwo onse amene sanalape ndi kulandira cikhululukiro ca macimo (Mateyu 25.41). Ndi malo a mkwiyo wa Mulungu ndi cilango ca macimo (2 Atesalonika 1.8-9).
- Yesu anatsikira kwa akufa kumvera mkwiyo wa Mulungu wa pa macimo kuti anthu ake sadzazunzika konse kotero. Anasiyidwa ndi Atate wake (kusiyidwa ndi Mulungu ndiko monga Gehena, Mateyu 27.45-46) kotero kuti anthu ake sadzasiyidwa ndi Mulungu ngakhale m'zowawa zoipa zoposa m'miyoyo yao (Salimo 94.14). Yesu ndi Wopambana.
- Fotokozani kuti onse amene akalibe kulandira Yesu kukhala Mbuye ndi Mpulumutsi wao iwo akamwalira (kapena pamene Yesu abwerera) adzatumidwa ku Gehena muyaya: kulibe thandizo koma mkwiyo wa Mulungu muyaya.

## 3. Tsiku lacitatu anaukanso kwa akufa – Kuwerenga Baibulo (30 minutes)
- Werengani pamodzi Mateyu 28.1-10 ndipo kambiranani pamodzi mafunso awa kapena alembeni pa bolodi ndipo uzani aphunzi kuwayankha m'magulu ang'ono.

**Mafunso**
1. Ndi yani amene anapita ku manda a Yesu?
2. Kodi mngelo anacita ciani atatsika Kumwamba?
3. Kodi mngelo anati ciani kwa akazi?
4. Kodi mngelo analamulira ciani akazi?
5. Kodi akazi anayankha bwanji?
6. Kodi akazi anakomana ndi yani pakubwerera kucokera ku manda?
7. Kodi Yesu anawauza ciani?

- Itakomana 10 minutes, kambiranani pamodzi mayankho. Mayankho abwino ali conco:
   1. **Ndi yani amene anapita ku manda a Yesu?**
      Yankho: Maria wa Magadala ndi Mariya wina.
   2. **Kodi mngelo anacita ciani atatsika Kumwamba?**
      Yankho: Anakunkhuniza mwala kucotsa pa citseko nakhala pamwamba pace.
   3. **Kodi mngelo anati ciani kwa akazi?**
      Yankho: Musaope inu, pakuti ndidziwa inu muli kufuna Yesu amena anapacikidwa. Iye mulibe muno iai; pakuti anauka, monga ananena. Idzani muno mudzaone malo m'mene anagonamo Ambuye.
   4. **Kodi mngelo analamulira ciani akazi?**
      Yankho: Ndipo pitani msanga, muuze ophunzira ace, kuti Wauka kwa akufa, ndipo onani, akutsogolerani ku Galileya; mudzamuona Iye komweko; onani ndakuuzani inu.
   5. **Kodi akazi anayankha bwanji?**
      Yankho: Anakondwera ndipo anamvera.
   6. **Kodi akazi anakomana ndi yani pakubwerera kucokera ku manda?**
      Yankho: Yesu yemwe.
   7. **Kodi Yesu anawauza ciani?**
      Yankho: Musaope; pitani, kauzeni abale anga kuti amuke ku Galileya, ndipo adzandiona Ine kumeneko.

- Mangiririrani ndi kunena kuti tikumbukira kuuka kwa Yesu caka ciriconse pa tsiku la Paska.

## 4. Game (optional, 10 minutes)

- Lembani pa bolodi.

| | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| Y | A | L | A | W | M | A | N | D | A |
| K | E | A | M | B | U | Y | E | P | N |
| U | R | S | C | A | I | Z | A | K | A |
| M | I | M | U | B | H | T | W | G | U |
| W | O | Y | P | A | M | T | D | F | K |
| A | A | L | E | L | U | R | N | P | A |
| M | F | A | E | E | N | A | O | A | D |
| B | U | C | Y | G | O | W | K | I | M |
| A | K | U | H | T | N | A | U | N | H |
| M | A | P | A | Z | I | M | K | U | K |

- Uzani aphunzi kupeza mau awa:

| | | |
|---|---|---|
| anauka | manda | Yesu |
| mngelo | akazi | kukondwa |
| mapazi | kumwamba | mantha |
| abale | Ambuye | akufa |
| inu | Iye | anthu |
| mwala | muno | apa |

## 5. Tsiku lacitatu anaukanso kwa akufa – umoyo wa masiku onse (30 minutes)

- Fotokozani kuti zonse zimene Yesu anacita, anazicita m'malo mwa anthu ake. Kodi kuuka kwa Yesu kutanthauza ciani kwa anthu ake?
  1. Yesu aukitsa anthu ake ku imfa ya uzimu (umoyo wopanda Mulungu, Aefeso 2.5). Iwo alandira umoyo wauzimu cifukwa ca kuuka kwa Yesu (Aefeso 2.1-10, Aroma 5.10, Akolose 2.13). Ici cichedwa 'kubadwa mwatsopano' (1 Petro 1.3, Yohane 3.7, Yohane 1.13).
  2. Yesu amathandiza anthu kukhala miyoyo yao yokondweretsa Mulungu. Anthu a Mulungu aitanidwa kusakhala m'uchimo (Aroma 6.12-13). Iwo akonzedwanso mwatsopano kotero kuti iwo sakondabe kucimwa koma akonda kumvera Mulungu (Akolose 3.10, Aefeso 4.23-24, Aroma 12.2). Zindikirani kuti umoyo wao wakale wocimwa ukhoza kuwabvutitsa (Aroma 7.14-21) koma suwalamulirabe. Mwa mphamvu ya Yesu woukitsidwa, anthu ake amenyera uchimo wopezeka mwa iwo komanso m'dziko lowazungulira.
     Mwa mphamvu yogonjetsa ya Yesu, anthu ake aphunzira kucita zoyang'anana ndi zimene iwo ankacita: cinyengo – coonadi, cigololo – kukhala okhulupirika, ufiti – Mulungu yekha, udani – cikondi, cisiriro – thandizo, kudzikweza – kudzicepetsa.
  3. Yesu adzaukitsa anthu ace kukhala naye Kumwamba muyayaya (1 Akorinto 15.20). Anthu a Mulungu ali ndi cikhulupiriro conse cakuti adzakhala ndi moyo wamuyaya pamodzi ndi Iye pakuti Yesu ali ndi moyo. Sayenera kukayika.
- Tsindikirani kuti anthu sakonzedwanso mwa mphamvu zao koma mwa mphamvu ya Yesu wamoyo amene anagonjetsa chimo ndi imfa.

## 6. Kutsiriza (5 minutes)

- Fotokozani mwacidule zimene zaphunzitsidwa lero ndipo kambani pamodzi: *Ndikhulupirira Mulungu Atate wamphamvu wa mphamvu zonse, wakulenga za kumwamba ndi za pansi. Ndikhulupirira Yesu Kristu, Mwana wake wobadwa yekha, Ambuye wathu amene anapatsidwa ndi Mzimu Woyera, nabadwa mwa Mariya namwaliyo, nasautsidwa kwa Pontio Pilato, namwalira, naikidwa m'manda. Natsikira kwa akufa. Tsiku lacitatu anaukanso kwa akufa.*
- Pempherani.

## Phunziro 7 Nakwera Kumwamba, nakhala padzanja lamanja la Mulungu Atate wa mphamvu zonse, kucokera komweko adzadza kudzaweruza anthu amoyo ndi akufa.

Zofunikira pa nthawi yophunzitsa
- Baibulo
- Bolodi
- Coko

### 1. Kulandiridwa (5 minutes)
- Landirani onse.
- Pempherani.
- Fotokozani mwacidule zimene tinaphunzira za Yesu m'maphunziro apitao.


### 2. Nakwera Kumwamba – Kuwerenga Baibulo (20 minutes)
- Werengani pamodzi Mateyu 28.18-20. Fotokozani kuti mau awa ananenedwa ndi Yesu Iye asanapite Kumwamba. Funsani aphunzi kuti Yesu anapatsa lamulo lotani kulingana ndi ndime ya 19 ndiponso m'mene iwo amvera lamulo ilo.
  Yankho: Yesu afuna kuti uthenga wake ulalikidwa pa dziko lonse lapansi.
- Werengani pamodzi Macitidwe a Atumwi 1.6-11 ndipo kambani pamodzi mafunso awa:
  1. **Kodi Yesu analonjeza ciani anthu ake kulingana ndi ndime ya 8?**
     Yankho: Analonjeza kutuma Mzimu Woyera kuti iwo akhoza kukhala kumcitira umboni pa dziko lonse lapansi.
  2. **Kodi kukhala mboni ya Yesu kutanthauza ciani?**
     Yankho: Kufalitsa kuti Yesu ndiye Mwana wa Mulungu amene akhoza ndi kufuna kukhululukira macimo (Iye yekha ndiye Mpulumutsi) ndipo akhoza ndi kufuna kubwezera anthu m'ubwenzi wabwino ndi Mulungu.
  3. **Nanga inu mungakhale mboni ya Yesu? Kodi mungakhale mboni ya Yesu m'njira yotani?**
     Yankho: Tiyenera kulalikira Uthenga wa Yesu Mpulumutsi. Tiyenera kudziwa Ambuye Yesu kwa ife eni kuti tikhale mboni zake: sitikhoza kukhala mboni za Wina amene sitidziwa.
  4. **Ndi ciani cimene cinacitika kwa Yesu kulingana ndi ndime ya 9?**
     Yankho: Ananyamulidwa Kumwamba.
  5. **Kodi amuna obvala zoyera anali yani?**
     Yankho: Angelo.
  6. **Kodi angelo anati ciani kutonthoza ophunzira a Yesu?**
     Yankho: Anati kuti Yesu adzabweranso.
- Mangirirani ndi kunena kuti caka ciriconse pa tsiku la Kukwera Kumwamba tikumbukira kukwera kwa Yesu.

### 3. Nakhala padzanja lamanja la Mulungu Atate wa mphamvu zonse (15 minutes)
- Nchito ya Yesu ya pa dziko lapansi linatha (Yohane 19.30, Yohane 17.4). Anabwerera ku ulemerero wa Mulungu Kumwamba kumene Iye analandira ulemerero: ali pafupi ndi Mulungu.

- Yesu akhala pa dzanja lamanja la Atate wake (1 Petro 3.22, Ahebri 1.3, Marko 16.19). M'dziko la Israyeli, dzanja lamanja linaimirira cikondi ndi mphamvu (Salimo 118.16, Salimo 108.6, Salimo 16.11b, Salimo 139.10). Iwo amene anakhala pa dzanja lamanja la mafumu a Aisrayeli anali m'ulemu umodzimodzi, mphamvu imodzimodzi ndi ulemerero umodzimodzi monga mfumu yemweyo (mwacitsanzo 1 Mafumu 2.19, Salimo 45.9). Pamene Baibulo likamba kuti Yesu akhala pa dzanja lamanja la Atate, ici citanthauza kuti apezeka m'ulemu umodzimodzi, mphamvu imodzimodzi ndi ulemerero umodzimodzi monga Mulungu Atate. Mulungu Atate ndi Mulungu Mwana ndiwo amodzi.
- Kumwamba Yesu sapumula cabe, koma apangitsa nchito yake yotsiriza kukhala ndi mphamvu: akhazikitsa nchito yake yotsiriza m'aliyense amene ali ake (Citsanzo ca munthu amene ali m'ndende. Ngati woweruza aonjola munthu, munthuyo aweruzidwa kuti alibe mlandu ndi cilango ndipo kenaka zitseko za ndende ziyenera kutsegulidwa kuti wandende amasulidwa ndithu).
- Funsani aphunzi zimene Yesu acita pokhala Kumwamba.
  Yankho:
  1. Alamulira (Aefeso 1.20-22, 1 Akorinto 15.25. Yesu ali ndi mpamvu kuposa mdani aliyense (Salimo 110.1 ndi 2, Yohane 10.27-29).
  2. Atuma Mzimu wake Woyera kuphunzitsa anthu ocimwa kulapa (kumva cisoni, kuulula, kuleka) ndi kukhulupirira Yesu (Yohane 14.16-19, John 16.7-11, Macitidwe 2.33).
  3. Apemphera ndi kupembedzera anthu ake kwa Mulungu (Yohane 17.9, Yohane 17.20, Ahebri 7.25, 1 Yohane 2.1) ndipo awakonzekera malo Kumwamba (Yohane 14.2-3, Yohane 17.24)
- Aliyense amene ali mwa Kristu sayenera kuopa m'ciriconse cocitika. Mutu wathu ali Kumwamba ndipo cifukwa cace thupi la Yesu (anthu ake) sadzatha psiti (ganizirani munthu m'madzi: ngati mutu wake ali pamwamba, munthuyo sakhoza kumira)
- Anthu a Mulungu aitanidwa kukhala monga abadwa ya Kumwamba (Afilipi 3.20). Ici citanthauza kuthanga kufuna Ufumu wa Mulungu ndi kumumvera m'mbali zonse za umoyo.

## 4. Cithunzi ca kucita manyazi ndi kukweza kwa Yesu (10 minutes)

- Lembani cithunzi ici pa bolodi (cacikulu kwambiri) ndipo uzani aphunzi kuti cithunzici ndico njira ya kufotokozera nchito yodabwitsa ya Yesu.



- Fotokozani motero. Lolani aphunzi kulemba citanthauzo ca manambala pa bolodi kuti akhale otengako mbali.
  1. Yesu ndi Mwana wa Mulungu. Anakhala ndi Mulungu Kumwamba nthawi zonse (phunziro 2 ndi 4).

  Yesu anacitidwa manyazi pamene Iye:
  2. Anasiya ulemerero wa Kumwamba ndipo anakhala ngati Munthu (phunziro 4).
  3. Sanawerengedwe ndi anthu m'moyo wake wa pa dziko lapansi (phunziro 4).
  4. Anasautsidwa kwa Pontio Pilato (phunziro 4).
  5. Anafa pa mtanda (phunziro 5).

  Yesu anakwezedwa ndipo adzakwezedwa pamene Iye:
  6. Anauka kwa akufa (phunziro 6).
  7. Anabwerera Kumwamba nakhala pa dzanja lamanja la Mulungu Atate wamphamvu zonse (phunziro la lero).
  8. Adzabweranso kuweruza anthu onse ndi kukhazikitsa mofikapo Ufumu wake (phunziro la lero).

## 5. Kucokera komweko adzadza kudzaweruza anthu amoyo ndi akufa. (30 minutes)

- Kumbutsani aphunzi zimene angelo anauza ophunzira a Yesu Iye atakwera Kumwamba: Yesu amene walandiridwa kunka Kumwamba kucokera kwa inu, adzadza momwemo monga munamuona alinkupita Kumwamba (Macitidwe 1.11b).
- Funsani aphunzi ngati anamva kuti Yesu adzabweranso ndipo ngati anamva tero, afunseni zimene zidzacitika Iye asanabwerenso ndi akabwera kulingana ndi iwo.
  Yankho:
  - Yesu asanabwerenso: awerengereni Mateyu 24.4-14. Aloleni kuganizira zimene ziri kucitika pa dziko lapansi ndi m'miyoyo yathu: tsoka zimene Yesu anakamba ziri kucitika kulikonse. Ici citanthauza kuti Yesu ali pafupi. Khalani okonzeka, khalani oyanjanitsidwa ndi Iye!
  - Yesu akabweranso: awerengereni Matthew 24.29-35. Fupikitsani ndime izi (kuli ndime zina zambiri za m'Baibulo koma osaya kwambiri m'phunziro iri).
  - Yesu atabweranso: awerengereni Mateyu 25.31-34 ndi Mateyu 25.41. Fotokozani kuti Yesu adzaweruza. Adziwa zonse. Adziwa zimene ziri m'mitima yathu. Adziwa ngati tinkamumvera mokhulupirika m'miyoyo yathu. Ngati macimo athu anakhululukidwa ndi Iye tidzakhala naye Kumwamba. Ngati macimo athu sanakhululukidwe tidzakhala ndi Satana m'Gehena. Aliyense amene anakhala moyo adzaweruzidwa (Cibvumbulutso 20.11-15). Sikudzakhalabe kukambirana kapena cikhululukiro, koma ciweruzo comaliza cokhala cabe pa m'mene munakhala moyo (pamodzi ndi Yesu kapena kopanda Iye).
- Uzani aphunzi kuti Yesu adzabwera nthawi iriyonse. Kodi akonzeka? Njira yekha ya kukhala okonzeka kukumana ndi Mulungu ndi ya kukhala abwenzi a Mulungu mwa Yesu m'malo mwa kukhala adani ake (osalapa, osabadwa mwatsopano ndi kopanda cikhululukiro). Ngati ndife oyanjanitsidwa ndi Mulungu mwa Yesu, maina athu ndi olembedwa m'buku la moyo.
- Funsani aphunzi ngati dzina la munthu angacotsedwe m'buku la moyo ngati munthuyo acimwa.
  Yankho: Iai, anthu a Mulungu sangacotsedwe m'buku la moyo. Mulungu amasunga anthu ake mpaka muyayaya (Yohane 6.39, Yohane 10.28, Yohane 18.9). Pamene munthu wakhululukidwa, akhululukidwadi mpaka muyayaya. Ici sicitanthauza kuti anthu a

Mulungu akhoza kungokhala m'uchimo (onani m'phunziro 6). Pamene akhala m'macimo, iwo samvera Mulungu ndipo ici cikhala ndi zoturukamo zoipa koposa. Iwo ali okhululukidwa ndipo ayenera kuphunzira kukhala oyera pa maso pa Mulungu. Ngati akonda kucita zimene Mulungu atsutsa nazo, ici ndi cizindikiro cakuti ndithu sanakhululukidwe ndipo sali m'modzi wa anthu a Mulungu.

- Fotokozani kuti kubweranso kwa Yesu ndiko citonthozo cacikulu ca anthu ake, pakuti adziwa kuti Woweruza wao ndiye Bwenzi lao amene anawamasula kale. Adzawamasula konse kwa adani ao onse ndi kuwatenga naye m'cisangalalo ndi ulemerero zakumwamba.

## 7. Kutsiriza (5 minutes)

- Fotokozani mwacidule zimene zaphunzitsidwa lero ndipo kambani pamodzi: *I believe in God the Father, Almighty, Ndikhulupirira Mulungu Atate wamphamvu wa mphamvu zonse, wakulenga za kumwamba ndi za pansi. Ndikhulupirira Yesu Kristu, Mwana wake wobadwa yekha, Ambuye wathu amene anapatsidwa ndi Mzimu Woyera, nabadwa mwa Mariya namwaliyo, nasautsidwa kwa Pontio Pilato, namwalira, naikidwa m'manda. Natsikira kwa akufa. Tsiku lacitatu anaukanso kwa akufa nakwera Kumwamba, nakhala padzanja lamanja la Mulungu Atate wa mphamvu zonse, kucokera komweko adzadza kudzaweruza anthu amoyo ndi akufa.*
- Pempherani.

## Phunziro 8 Ndikhulupirira Mzimu Woyera

Zofunikira pa nthawi yophunzitsa
- Baibulo
- Bolodi
- Coko

## 1. Kulandiridwa (5 minutes)
- Landirani onse.
- Pempherani.
- Bwezerani mwacidule phunziro 7.
- Fotokozani kuti tinaphunzira za Mulungu Atate ndi Mulungu Mwana (Yesu). Lero tidzaphunzira za Mulungu Mzimu Woyera.

## 2. Mzimu Woyera – M'mene Iye aliri (20 minutes)
- Mangirirani mphunzi mmodzi ku maso. Lembani cithunzi pa bolodi ndipo funsani womangidwa ku maso kukuuzani cimene mwalemba. Adzalephera kuyankha. Fotokozani kuti onse a pa dziko lapansi ndiwo akhungu m'uzimu: olephera kuona m'mene Mulungu aona. Iwo otsegulidwa maso ndi Mulungu Mzimu Woyera akhoza kudzizindikira monga ocimwa, adziwa Mulungu monga woyera ndi wopanda banga ndiponso adziwa Yesu monga Mpulumutsi wao. Kopanda Mzimu Woyera ndife otayika m'uzimu. Baibulo litiphunzitsa kuti ndi Mulungu amene anafulumizitsa kupulumutsa anthu. Tikhulupirira ndipo ndife opulumutsidwa pakuti Iye atipangitsa ife kulapa ndi kumkhulupirira (Macitidwe 13.48, Atesalonika 2.13, Macitidwe 2.47).
- Fotokozani za Mulungu Mzimu:
  - Aphunzitsa anthu kulapa macimo ao (kumva cisoni, kuulula, kuleka) ndi kukhulupirira Yesu pa cipulumutso (Yohane 16.8-11, Zekariya 12.10, Macitidwe 10.34-48).
  - Mzimu Woyera atumidwa ndi Yesu (amene anatha zonse kuti anthu ocimwa apulumuke) ndipo apangitsa anthu kukhala ndi cikhulupiriro mwa Yesu. Zonse zofunikira kupulumuka zipatsidwa ndi Mulungu; ngakhale cikhulupiriro cipatsidwa ndi Iye (Aefeso 2.8). Ngati mufuna kuthandiza Mulungu kukupulumutsani, simudzapulumutsidwa! Koma apatsa kwaulere kwa iwo amene adalira konse pa cipulumutso cace cabe. Mulungu apereka zonse mwa cisomo. Mzimu Woyera akhoza kusintha wina aliyense, kulibe munthu amene ali wopanda ciyembekezo. Funsani Mulungu!
  - Akhala mwa anthu a Mulungu (mwacitzanzo 2 Akorinto 1.22, Agalatiya 4.6, Yohane 14.15-26). Awathandiza m'miyoyo yao ya uzimu ndi miyoyo ya masiku onse, akhala nao nthawi zonse, awayeretsa, awakonzanso m'cifanizo ca Mulungu ndipo awalimbikitsa kukhala mboni za Yesu.
- Mangirirani ndi kunena kuti Mzimu Woyera ali monga nyali younikira mdima: nyali siidziunikira, koma cimene ciunikiridwa ndi cirangali. Mzimu Woyera safuna kukopa anthu kwa Iye yemwe, koma kwa Yesu Kristu: m'mene Yesu aliri ndi zimene Iye anacita (Yohane 16.13-14).

## 4. Mzimu Woyera – Kuwerenga Baibulo – Bible study (30 minutes)
- Werengani pamodzi Yohane 15.26-27 ndipo fotokozani kuti ndife oitanidwa kukhala mboni za Yesu. Tiyenera kufalitsa Uthenga wa Yesu. Mulungu Mzimu Woyera

akonzekeretsa anthu kucita tero. Mzimu Woyera ucitira mboni Yesu ndipo akonzekera anthu a Mulungu kucitiranso umboni Yesu.

- Werengani pamodzi Macitidwe 2.1-13 ndipo yankhani mafunso awa pamodzi kapena m'magulu.

**Mafunso**
1. Kodi linali tsiku lanji kulingana ndi ndime ya 1?
2. Chulani zinthu zitatu zimene zinacitika pa tsiku la Pentekoste zopezeka m'ndime za 2-4.
3. Ndi ciani cimene cinacitika pamene anthu anamva ophunzira kulankhula zilankhulo zosiyana-siyana, kulingana ndi ndime ya 7?
4. Kodi ophunzira a Yesu analankhulira ciani m'zilankhulo zosiyana-siyana?
5. Kodi anthu anayankha bwanji pomvera ophunzira kulankhula zilankhulo zosiyana-siyana?

- Itakomana 10 minutes kambiranani pamodzi mayankho. Mayankho abwino ali conco:
  1. **Kodi linali tsiku lanji kulingana ndi ndime ya 1?**
     Yankho: Tsiku la Pentekoste.
  2. **Chulani zinthu zitatu zimene zinacitika pa tsiku la Pentekoste zopezeka m'ndime za 2-4.**
     Yankho:
     1. Kunamveka mau ngati mphepo yolimba (ndime ya 2). Zindikirani kuti kunali cabe *mau* ngati mphepo. Baibulo lifanizira Mzimu Woyera ndi mpempho kaamba ka mphamvu ndi kusaoneka kwa mphepo ndi Mzimu Woyera.
     2. Kunaoneka malilime ogawanikana onga amoto omwe anakhala pa ophunzira (ndime ya 3). Zindikirani kuti kunalibe moto woona koma *kunaoneka* monga moto. M'Baibulo kawirikawiri moto ndi cizindikiro ca kupezeka kwa Mulungu ndi ciyero cimene cisakaza zosayeretsedwa zonse (mwacitsanzo Eksodo 3.2, Eksodo 19.18, Yesaya 66.15, Ahebri 12.29). Malilime ogawanikana onga amoto angakhale cizindikiro ca kulalikidwa koyera ndi kamphamvu kwa Uthenga wa Yesu.
     3. Ophunzira anadzazidwa ndi Mzimu Woyera nalankhula ndi malilime ena (ndime ya 4).
        Aliyense pafupi nao anakhoza kumvetsetsa zimene anakamba za Yesu. Aliyense anayenera kumvera uthenga wabwino wa Yesu Kristu. Tiziuza aliyense za Iye.
        Zindikirani kuti zimene zinacitika pa tsiku la Pentecost ndizo zosiyana ndi zimene timacha 'kukamba malilime'. Pa tsiku la Pentecost ophunzira analankhula zilankhulo zosiyanasiyana ndi colinga cakuti aliyense akhoza kumvetsa zimene zakambidwa. Masiku ano pamene timvera za 'kukamba malilime' amakamba cilankhulo cosamveka cobweretsa msokonezo. Cifukwa cace:
        - Kukamba malilime ndi cimene cicitika pakati pa munthu ndi Mulungu kumlemekeza Mulungu (1 Akorinto 14.2, 1 Akorinto 14.28)
        - Tiziyesetsa kulankhula zimene zipindulira anthu ena ndipo cifukwa cace tiyenera kulankhula zimene iwo amvetsa (1 Akorinto 14.9, 1 Akorinto 14.12-13, 1 Akorinto 14.18-19)
        - Kufotokoza ndi kuyesa zimene zakambidwa m'malilime ndiko kofunikira kwambiri (1 Akorinto 14.26-29)
  3. **Ndi ciani cimene cinacitika pamene anthu anamva ophunzira kulankhula zilankhulo zosiyana-siyana, kulingana ndi ndime ya 7?**
     Yankho: Anasokonezeka pakuti anamva ophunzira kulankhula m'cilankhulo ca cibadwidwe cao

4. **Kodi ophunzira a Yesu analankhulira ciani m'zilankhulo zosiyana-siyana?**
   Yankho: Nchito zodabwitsa za Mulungu (kupulumutsidwa kwa anthu mwa Yesu Kristu). Onani kuti Mzimu Woyera apangitsa anthu kuganizira Yesu osati Iye yemwe (monga m'citsanzo ca nyali).
5. **Kodi anthu anayankha bwanji pomvera ophunzira kulankhula zilankhulo zosiyana-siyana?**
   Yankho: Ena anakayikira citanthauzo ndipo ena ananyoza.

- Werengani pamodzi Macitidwe a Atumwi 16.16-18 ndipo yankhani mafunso awa pamodzi kapena m'magulu.

**Mafunso**

6. Werenganinso ndime ya 16. Kodi Paulo ndi anzake anakomana ndi yani pamene anali kunka kukapemphera?
7. Kodi namwaliyo anali kupeza bwanji ndalama?
8. Kodi namwaliyo ananena ciani pamene analondola Paulo ndi anzake?
9. Kodi ndi zoona kuti Paulo ndi anzake anali akapolo a Mulungu ophunzitsa za cipulumutso?
10. Kodi Paulo analamulira ciani mzimuwo?
11. Kodi ici citanthauza kuti mzimu unali wabwino kapena woipa? Kodi Baibulo litiuza ciani za kukhala ndi mzimu wam'bwebwe?
12. Kodi ndi cotheka kuti mzimu woipa udzionetsa ngati mzimu wabwino?
13. Kodi kusiyana kwa Mzimu Woyera ndi mizimu ina yonse ndi kotani?

- Itakomana 10 minutes kambiranani pamodzi mayankho. Mayankho abwino ali conco:

6. **Werenganinso ndime ya 16. Kodi Paulo ndi anzake anakomana ndi yani pamene anali kunka kukapemphera?**
   Yankho: Anakomana ndi namwali amene anali ndi mzimu wambwebwe.
7. **Kodi namwaliyo analipeza bwanji ndalama?**
   Yankho: Anapeza ndalama mwa kulosha ndi kunena za tsogolo.
8. **Kodi namwaliyo ananena ciani pamene analondola Paulo ndi anzake?**
   Yankho: Ananena kuti iwo ndiwo akapolo a Mulungu olalikira njira ya cipulumutso.
9. **Kodi ndi zoona kuti Paulo ndi anzake anali akapolo a Mulungu ophunzitsa za cipulumutso?**
   Yankho: Inde, ndi zoona.
10. **Kodi Paulo analamulira ciani mzimuwo?**
    Yankho: Analamulira mzimuwo kuturuka m'namwaliyo m'dzina la Yesu.
11. **Kodi ici citanthauza kuti mzimu unali wabwino kapena woipa? Kodi Baibulo litiuza ciani za kukhala ndi mzimu wam'bwebwe?**
    Yankho: Mzimuwo unali woipa. Mulungu safuna anthu ake kukhala ndi mzimu wam'bwebwe (mwacitsanzo Deuteronomo 18.10-11).
12. **Kodi ndi cotheka kuti mzimu woipa udzionetsa ngati mzimu wabwino?**
    Yankho: Inde, ndi cotheka. Ngakhale Satana akhoza kudzionetsa ngati mngelo wa kuunika (2 Akorinto 11.14). Tiyenera kukhala ocenjera kwambiri ndi kuyesa zonse (1 Yohane 1.1-3).

13. **Kodi kusiyana kwa Mzimu Woyera ndi mizimu ina yonse ndi kotani?**
    Yankho:
    - Mzimu Woyera ndi **Mulungu** (mwacitsanzo 2 Akorinto 13.14). Mulungu Atate, Mulungu Mwana ndi Mulungu Mzimu Woyera ndiwo m'modzi.
    - Mzimu Woyera **alemekeza Yesu** (Yohane 16.14). Aunikira anthu kotero kuti iwo alapa macimo ao ndi kukhulupirira Yesu. Adziwitsa anthu zonse za Yesu, osati Yesu amene anacita zodabwitsa cabe. Aphunzitsa anthu za Yesu monga:
        - Mpulumutsi. Yesu, Mwana wa Mulungu, anadza pa dziko lapansi. Anazunzika, anafa pa mtanda ndi kuuka kwa akufa kukhululukira macimo. Njira yeni-yeni yobwezeretsedwamo m'ubwenzi wabwino ndi Mulungu ndi mwa Yesu. Colinga ca Yesu cinali kubweretsanso anthu m'ubwenzi wabwino ndi Mulungu mwa kukhululukira macimo ao. Colinga ca Yesu si cakuti ife tikhale ndi moyo wosangalala ndi wopanda bvuto.
        - Ambuye. Yesu alamulira dziko lonse lapansi. Alamulira anthu ake. Awayeretsa kotero kuti iwo akhala m'mene Mulungu afuna iwo kukhala. Aphunzitsa anthu kulemekeza Mulungu m'miyoyo yao.
    - Mzimu Woyera ndi **wopatulika kwa zoipa** (Aroma 8.5, 1 Akorinto 6.10 ndi 11). Mzimu Woyera atsutsana ndi uchimo ndipo ayeretsa anthu ku uchimo (Aroma 8.16). Mizimu ina sisamalira ngati anthu akhala m'macimo. M'malo mwake mizimu iyo ilimbitisa mitima ya anthu kukhala m'macimo, mwacitsanzo kukonda ndalama (1 Timoteo 6.10), kudzikuza (Salimo 138.6), kufufuza zinthu zauzimu (Levitiko 19.31, Yesaya 8.19, Levitiko 2.27, Deuteronomo 29.29) ndi kuphunzitsa mabodza (1 Timoteo 4.1-3).
    - Ndi Mzimu Woyera yekha amene abalitsa anthu **zipatso za uzimu** (Agalatiya 5.22-23). Mizimu yoipa akondwera poona kuti anthu akhala aneneri onyenga (Mateyu 7.15, 1 Yohane 4.1), aziphunzitsi onama (2 Petro 2.1), ocita zodabwitsa zonyenga (Mateyu 24.24) ndi kulalikira uthenga wabodza (Agalatiya 1.6 ndi 7). Koma mizimu yoipa siikhoza kubalitsa zipatso zabwino m'miyoyo ya anthu. Zipatsozo zicokera kwa Mulungu Mzimu pakuti Iye akonzanso ndi kuyeretsa anthu (1 Petro 1.2, 1 Akorinto 6.11, Aroma 8.13). Cifukwa cace tiyenera kuyang'anira zipatso za m'moyo mwa munthu. Kodi iwo aonetsa cikondi, cimwemwe, mtendere, kuleza mtima, cifundo, kukoma mtima, cikhulupiriro, cifatso ndi ciletso?
      Funsani aphunzi ngati azindikira zipatso zauzimu m'miyoyo yao. Ngati inde, lemekezani Mulungu pa zimene anakupatsani. Ngati iai, pemphani Mulungu kuti Mzimu wake Woyera kuphunzitseni. Afuna kukupatsani Mzimuyo (Luka 11.13)

- Awerengereni aphunzi <u>Macitidwe 2.21</u> ndipo fotokozani kuti mau awa ananenedwa ndi Petro pa tsiku la Pentekoste. Fotokozani citanthauzo ca ndime iyi ya m'Baibulo. Kuitana Ambuye kutanthauza kukhala ndi cikhulupiriro ndiponso kuika ciyembekezo ca cipulumutso ca macimo mwa Iye yekha. Ciyembekezo cathu si kulapa kwathu, pemphero lathu kapena miyoyo yathu yodzipereka, koma Yesu!
- Uzani aphunzi kuti caka ciriconse pa tsiku la Pentekoste timakumbukira kuti Yesu anatuma Mzimu wake Woyera.

## 5. Kutsiriza (5 minutes)

- Fotokozani mwacidule zimene zaphunzitsidwa lero ndipo kambani pamodzi: *I believe in God the Father, Almighty, Ndikhulupirira Mulungu Atate wamphamvu wa mphamvu zonse, wakulenga za kumwamba ndi za pansi. Ndikhulupirira Yesu Kristu, Mwana wake wobadwa yekha, Ambuye wathu amene anapatsidwa ndi Mzimu Woyera, nabadwa mwa*

*Mariya namwaliyo, nasautsidwa kwa Pontio Pilato, namwalira, naikidwa m'manda. Natsikira kwa akufa. Tsiku lacitatu anaukanso kwa akufa nakwera Kumwamba, nakhala padzanja lamanja la Mulungu Atate wa mphamvu zonse, kucokera komweko adzadza kudzaweruza anthu amoyo ndi akufa. Ndikhulupirira Mzimu Woyera. Ndikhulupirira Mpingo wopatulika wa Kristu wa kwa anthu onse.*

- Pempherani.

**Phunziro 9 Ndikhulupirira Mpingo wopatulika wa Kristu wa kwa anthu onse, ciyanjano ca oyera mtima, kukhululukidwa kwa macimo**

Zofunikira pa nthawi yophunzitsa
- Baibulo
- Bolodi
- Coko

## 1. Kulandiridwa (5 minutes)
- Landirani onse.
- Pempherani.
- Fotokozani mwacidule zimene zinaphunzitsidwa m'phunziro 8.

## 2. Ndikhulupirira Mpingo wopatulika wa Kristu wa kwa anthu onse (20 minutes)
- Funsani aphunzi ngati amapita ku calichi. Ngati inde, afunseni cifukwa ciani amapita.
- Fotokozani kuti mpingo utanthauza: gulu la anthu osonkhanidwa ndi Mulungu amene ali ake. Gwiritsani nchito citsanzo ca banja: banja liri ndi mamembala amene apanga pamodzi banja. Ana a Mulungu apanga pamodzi mpingo wa Mulungu.
- Afunseni ngati kupita ku calichi kupangitsa munthu kukhala Mkristu woona.
  Yankho: Iai. Cimodzimodzi monga kupita ku malo ophikira buledi sikukusandulitsani mkate kapena kupita ku malo okonzera magalimoto sikukusandulitsani galimoto. Ndi cotheka kuti anthu ena amabwera ku calichi (nyumba) koma sapezeka m'banja la Mulungu (mpingo, eklesia). Citsanzo: ngati anthu okhala pafupi nanu abwera kucezera nikhala pafupi nanu, sasandulika membala wa banja lanu.
- Awerengereni aphunzi Yohane 10.14-16 ndipo fotokozani kuti Yesu (osati azibusa kapena aneneri) asonkhanitsa, ateteza ndi kusunga anthu ake (Macitidwe 20.28, Mateyu 16.18, Akolose 1.18). Iye akulitsa mpingo wake mwa Mau ake (Baibulo) ndi Mzimu wake Woyera amene aphunzitsa anthu kulapa ndi kukhulupirira Yesu kuti akhale mamembala a banja la Mulungu (Aroma 1.16, Aroma 10.14-17, Macitidwe 2.42-47). Cifukwa cace nchito yofunikira koposa ya azibusa ndiyo kuphunzitsa Baibulo.
- Mpingo wa Mulungu uli *wopatulika*: ukhala ndi anthu amene apatulidwa ndi Mulungu kukhala ake, kumlemekeza ndi kumumvera (Aefeso 5.27, Aefeso 1.4).
- Mpingo wa Mulungu uli wa kwa anthu onse: banja la Mulungu likhala ndi anthu a ku dziko lonse lapansi amene ali ake opezeka m'macalichi ambiri osiyanasiyana (Cibvumbulutso 5.9, 1 Akorinto 1.2).

## 3. Ciyanjano ca oyera mtima (20 minutes)
- Funsani aphunzi 'woyera mtima' ndi ciani.
  Yankho: Munthu wopatulidwa ndi Mulungu kukhala wake, munthu woyera woyeretsedwa ku macimo ake ndi Mulungu, munthu amene ali wopatuka ndi dziko lapansi cifukwa ca kukhulupirira Yesu (1 Akorinto 6.10-11, 1 Akorinto 1.2, Aefeso 2.19).
- Woyerayo mwana wa Mulungu akhozabe kucimwa (Agalatiya 5.17, Aroma 7.18, 1 Yohane 1.8). Si ndife oyenerera mpaka tafika Kumwamba. Tsiku lirilonse tifunika Yesu kutiyeretsa (1 Yohane 1.7, 1 Yohane 1.9, Salimo 19.12).
  Ici sicitanthauza kuti ndi kobvomerezedwa ngati mwana wa Mulungu amakhala m'uchimo nthawi zonse (Aroma 6.1-2, Aroma 6.14-15). Iwo okhululukidwa macimo ao, amakonda

Mulungu kaamba ka mphatso yaikulu ya cikhululukiro mwa mwazi wa Yesu Mwana wake. Cifukwa cace iwo safuna kusamvera Mulungu mwa kucimwa.
Iwo okonda kukhala m'uchimo ndi osamenya uchimo, aonetsa kuti sanakhululukidwe konse (1 Yohane 1.6, Yuda 1.4, Aroma 3.8, 1 Petro 2.16).

- Funsani aphunzi kuti 'ciyanjano' ndi ciani.
  Yankho: Ubwenzi wogwirizana kwambiri.
- Anthu a Mulungu ayanjana ndi:
  1. Mulungu yemwe (1 Yohane 1.3, 1 Akorinto 1.9, Yohane 17.21, Yohane 14.23). Iwo ali anthu *ake*; ndiwo a Kristu. Mulungu alankhula nao mwa Baibulo ndipo iwo alankhula naye mwa pemphero. Iwo asanapulumutsidwe ndi Yesu, anakhala kutali ndi Mulungu koma tsono ali pafupi (Aefeso 2.13).
  2. Wina ndi mnzace (1 Yohane 1.3, 1 Yohane 1.7, Aefeso 2.19). Ali m'banja la Mulungu; abale ndi alongo. Ali abale ndi alongo pakuti Mulungu ndiye Tate wao mwa Yesu amene anawabweretsa m'banja la Mulungu. Ici sicitanthauza kuti aliyense amene adziitana mbale kapena mlongo, apezekadi m'banja la Mulungu, koma cabe iwo amene abadwa mwa Mzimu (Yohane 3.6).
- Funsani aphunzi kuti Akristu obadwa mwatsopano ayanjana m'njira yotani.
  Yankho: Mwacitsanzo mwa kulimbikitsana, kutsutsana, kuphunzitsana, kukondana, kuthandizana, kupemphera pamodzi, kuwerenga Baibulo pamodzi, kumenyera nkhondo ya Satana ndi uchimo pamodzi.

## 4. Sewero (15 minutes)

- Lembani mutu pa bolodi (wopanda maso, makutu, mphuno ndi malilime).
- Funsani aphunzi ena kulemba zigawo zolumikizika za mutu womwe mwalemba.
- Fotokozani kuti zigawo zonse zisiyana. Zigawo zina zioneka bwino, zina sizioneka bwino. Fotokozani kuti Akristu onse asiyana: tisiyana ku mbali ya makhalidwe, ziyambi zathu ndi zimene tikhoza kucita bwino. Komabe tiyenera kukonda aliyense m'banja la Mulungu monga mbale/mlongo, pakuti Mulungu Tate wathu ndi Mutu wathu awakonda.
- Kukafotokoza bwino werengerani aphunzi <u>1 Akorinto 12.12-26</u> ndipo fotokozani kuti mgwirizano ndi wofunikira kwambiri (mgwirizano m'Kristu pakuti Kristu ndiye Pakatipakati. Kulibe mgwirizano ndi iwo amene akanira ziphunzitso zambiri zofunikira za m'Baibulo).

## 5. Kukhululukidwa kwa macimo (30 minutes)

- Funsani aphunzi citanthauzo ca chimo.
  Yankho:
  - <u>Kucimwa kutanthauza kusamvera Mulungu ndi kucita zimene Mulungu aletsa</u>. Mulungu adziwa zonse: macitidwe athu, mau athu ndi maganizo athu (Macitidwe 1.24, Hebri 4.13, Miyambi 15.3, Salimo 44.23).
  - <u>Aliyense anabadwa ndi mtima wocimwa: tinabadwa ndi cifuniro cofuna kudzikondweretsa osati Mulungu.</u> Baibulo likamba kuti magwero (ciyambi) a miyoyo yathu aturuka m'mitima yathu (Miyambi 4.23). Kamvekedwe, zilakolako ndi maganizo zicokera m'mitima yathu. Aliyense acimwa, cimene citanthauza kuti aliyense anabadwa nao mtima wocimwa (Yobu 15.14, Aroma 5.12, 1 Yohane 1.8). Aliyense anabadwa ndi kamvekedwe, zilakolako ndi maganizo zotsutsa zimene Mulungu afuna. Ici citanthauza kuti zonse zimene ticita ndi zodetsedwa ndi uchimo. Ndife auchimo konse, osati pang'ono cabe. Cifukwa cace aliyense ali wolakwa ndi pansi pa ciweruzo ca Mulungu (Aroma 3.10-19, Aroma 3.23).

- Ndife ocimwa konse ndipo tifunika Yesu kutipulumutsa konse. Anthu ena aganiza kuti si ndiwo oipa kwambiri. Aganiza kuti tikwanitsa komanso kuti tiyenera kudzifikitsa cilungamo ndi ciyero mwa pemphero ndi kudzilimbitsa. Aganiza kuti Yesu amaliza zimene tisowa: ticita zonse zatheka kukhala monga mwa muyeso wa Mulungu ndipo Yesu amaliza pamene tilephera. Ici si cimene Baibulo liphunzitsa. Baibulo liphunzitsa kuti Yesu alungamitsa ndi kuyeretsa anthu mwa kucotsa macimo ao (Aroma 3.24, Aroma 5.19, 1 Akorinto 6.11, Yesaya 53.11). Baibulo sitiphunzitsa kuti Mulungu ndi anthu agwira nchito pamodzi kuti apulumutse anthu (kumbukirani phunziro 1 ndi 5 m'mene tinaphunziramo kuti ndife akufa m'uzimu ndiponso kuti umoyo wauzimu ndiwo mphatso). Ndife olungama ndi oyera cifukwa ca kukhala *mwa* Yesu, osati cifukwa ca kucita zatheka. Tiyenera kudzicepetsa ndi kubvomera kuti tilibe ciyembekezo ciriconse ca cipulumutso mwa ife mwini.

- Fotokozani cotsatira ca chimo lirilonse m'miyoyo yathu.
  - Tiyenera mkwiyo wa Mulungu (Aroma 3.10-19). Cifukwa ca kusamvera kwathu ndife olakwa ndipo tiyenera kulangidwa.
  - Ndife otembereredwa ndi Mulungu (Agalatiya 3.10). Tinataya cikhulupiriro ca Mulungu ndi citetezo cace ndipo tsono tiribe mphamvu ndipo ndife osatetezeka.
  - Mulungu atituma kutali kwa Iye (Mateyu 7.23, Mika 3.4). Tadzicitira manyazi. Ndife osakondwera kwambiri, odetsedwa ndi aumphawi m'uzimu.
- Funsani aphunzi citanthauzo ca cikhululukiro.

  Fotokozani kuti cikhululukiro citanthauza kuti cifukwa ca Yesu, Mulungu acotsa macimo a munthu wina wace ndipo saganiziranso macimowo.

  Wocimwa ali pansi pa mkwiyo wa Mulungu, wotembereredwa ndi wolekanitsidwa ndi Mulungu. Cina cace ciyenera kucitika kuti Mulungu akhute. Yesu Mwana wosacimwa wa Mulungu ndiye yekha amene anakhoza kukhutitsa Mulungu, pakuti Iye ananyamula macimo nafa pa mtanda kubwezeretsa zotsatira ca macimo. Cikhululukiro sicitanthauza kuti Mulungu angoiwala cifukwa ca cifundo cace, koma citanthauza kuti Iye wolungama ndi woyera ali wokhutidwa ndithu ndi zimene zinacitika. Yesu ndiye Mpulumutsi wonse wa munthu wocimwa konse. Sitithandiza m'cipulumutso cathu!
  - Yesu akhoza ndi kufuna kucotsa mkwiyo wa Mulungu wa pa ife (1 Atesalonika 1.10, Aroma 5.9-10). Ngati tiri mwa Yesu, ndife omasuka!
  - Akhoza ndi kufuna kucotsa temberero la Mulungu la pa ife (Agalatiya 3.13). Ngati tiri mwa Yesu, Mulungu wa makamu ndiye Tate wathu ndipo sitiyenera kuopa!
  - Akhoza ndi kufuna kutibweretsa m'ubwenzi wabwino ndi Mulungu (Aefeso 2.13, 1 Petro 3.18). Ngati tiri mwa Yesu, ndife ana a Mulungu amene ali pafupi naye!
- Aliyense wokhululukidwa ndi Yesu ndiye woyera. Akhoza kucimwa koma safuna kukhalabe m'uchimo (onani mbali ya 3). Pamene chimo linacitidwa, cofunikira kwambiri ndico kuliulula kwa Mulungu, kulapa ndi kupempha cikhululukiro.

## 6. Cikhululukiro ca macimo – Mulungu wokhululukira – Kuwerenga Baibulo (20 minutes)

- Werengani pamodzi Salimo 130 ndipo yankhani mafunso awa pamodzi kapena m'magulu ang'ono.

**Mafunso**
1. Kodi mozama ndi ciani (ndime ya 1)?
2. Cifukwa ciani wolembera salimo iri anapfuulira Yehova?
3. Werenganinso ndime ya 3 ndipo yankhani funso iri, 'Ndani adzakhala ciriri ngati Mulungu asunga mphulupulu zathu?'
4. Kodi cikhululukiro cicokera kuti? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
5. Kodi tiyenera kucita ciani kuti tilandire cikhululukiro?

- Itakomana 10 minutes kambiranani pamodzi mayankho. Mayankho abwino ali conco:
  1. **Kodi mozama ndi ciani (ndime ya 1)?**
     Yankho: Zocitika zacisoni, mabvuto, macimo.
  2. **Cifukwa ciani wolembera salimo iri anapfuulira Yehova?**
     Yankho: Mulungu yekha anali ciyembekezo cace.
  3. **Werenganinso ndime ya 3 ndipo yankhani funso iri, 'Ndani adzakhala ciriri ngati Mulungu asunga mphulupulu zathu?'**
     Yankho: Kulibe amene adzakhala ciriri (Aroma 3.23).
  4. **Kodi cikhululukiro cicokera kuti? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?**
     Yankho: Kwa Mulungu (ndime ya 4). Cikhululukiro ndico mphatso imene sitingakwanitse mwa mphamvu yathu mwa kucita zabwino koma ndiyo cinthu cimene tilandira kwa Mulungu mwa Yesu Kristu.
  5. **Kodi tiyenera kucita ciani kuti tilandire cikhululukiro?**
     Yankho: Kuyembekezera Mulungu (ndime ya 5) (1 Yohane 1.9).
     1. Kulapa macimo athu (kumva cisoni, kuulula chimo lathu lirilonse, kuleka kuwacita).
     2. Kupempha Mulungu kutikhululukira mwa Yesu Kristu Mpulumutsi.
     3. Kukhulupirira Yesu (kudalira pa cipulumutso cace, kudzipereka kwa Iye)

## 8. Kutsiriza (5 minutes)

- Fotokozani mwacidule zimene zaphunzitsidwa lero ndipo kambani pamodzi: *I believe in God the Father, Almighty, Ndikhulupirira Mulungu Atate wamphamvu wa mphamvu zonse, wakulenga za kumwamba ndi za pansi. Ndikhulupirira Yesu Kristu, Mwana wake wobadwa yekha, Ambuye wathu amene anapatsidwa ndi Mzimu Woyera, nabadwa mwa Mariya namwaliyo, nasautsidwa kwa Pontio Pilato, namwalira, naikidwa m'manda. Natsikira kwa akufa. Tsiku lacitatu anaukanso kwa akufa nakwera Kumwamba, nakhala padzanja lamanja la Mulungu Atate wa mphamvu zonse, kucokera komweko adzadza kudzaweruza anthu amoyo ndi akufa. Ndikhulupirira Mzimu Woyera. Ndikhulupirira Mpingo wopatulika wa Kristu wa kwa anthu onse, ciyanjano ca oyera mtima, kukhululukidwa kwa macimo.*
- Pempherani.

## Phunziro 10 Kuukanso kwa thupi, ndi moyo wosatha. Amen.

<u>Zofunikira pa nthawi yophunzitsa</u>
- Baibulo
- Bolodi
- Coko

## 1. Welcome (5 minutes)
- Landirani onse.
- Pempherani.
- Fotokozani mwacidule zimene zinaphunzitsidwa m'phunziro 9.

## 2. Kuukanso kwa thupi (20 minutes)
- Funsani aphunzi kuti ndi ciani cimene cicitika tikamwalira.
- Fotokozani kuti:
  - Mzimu wathu upita mosacedwa Kumwamba kapena ku Gehena (Luka 16.22-23, Luka 23.43). Kulibe malo kumene munthu wakufa angayeretsedwe ku macimo ake. Cifukwa cace tiyenera kuyesa miyoyo yathu yofunikira kwambiri: miyoyo yathu iri cokonzekero kaya Kumwamba kapena Gehena.
  - Matupi athu adzaikidwa m'manda (mungakambirane miyambo ya maliro: kukambirana ncifukwa ciani anthu amasunga miyambo yotero ndiponso kuiweruza kulingana ndi Baibulo. Osatenga nthawi yaitali koma dziwitsani aphunzi kuti Baibulo ndi tsogoleri lathu m'zonse).
- M'phunziro 7 tinaphunzira kuti Yesu adzabweranso. Akabweranso Yesu, anthu akufa adzaukitsidwa. Aliyense, pakuti njira m'mene munthu anamwalira siyofunikira. Mulungu ali ndi mphamvu kuukitsa wina aliyense.
- Aliyense atafa aweruzidwa mosacedwa (onani pamwamba) koma aliyense adzaweruzidwanso pamene Yesu abweranso (onani Phunziro 7, Civumbulutso 20.12). Ciweruzo coyamba ndico pa yekha ndipo caciwiri cidzacitika pa gulu: aliyense adzaona ulemerero wa Mulungu, cilungamo cace ndi cifundo cace ca kwa anthu ake. Ici sicitanthauza kuti ciweruzo caciwiri cingasiyane ndi ciweruzo coyamba. Kulibe mpata kupulumutsa titamwalira.
- Fotokozani kuti thupi la wina aliyense lidzasinthika (1 Akorinto 15.42-44).
  - Matupi a anthu a Mulungu adzasinthika kotero kuti ali monga thupi lolemekezeka la Yesu (Afilipi 3.21).
  - Matupi a iwo amene anafa kopanda Yesu adzasinthika kotero kuti akhoza kupirira zowawa ku Gehena muyaya (Mateyu 10.28, Marko 9.48).
- Fotokozani kuti mathupi athu ndi mizimu yathu zidzayanjanitsidwa kukhala Kumwamba kapena ku Gehena nthawi zonse. Matupi athu ali ofunikira pa maso pa Mulungu monga mizimu yathu. Cifukwa cace tiyenera kusamalira matupi athu!

### 3. Ndi moyo wosatha – Kuwerenga Baibulo (20 minutes)

*Ophunzira angakhale ndi mafunso a anthu 144.000 opezeka m'Civumbulutso 14.1. Akristu asiyana pa zimene aganiza za nambala iyi cifukwa ca zifukwa zosiyana. Cifukwa cace osatenga nthawi ikulu kukambiranako. Tsindikirani kuti buku la Cibvumbulutso ndilo buku la uneneri. Tiyenera kukhala maso pa kumasulira mfundo.*
*Buku la Cibvumbulutso likamba za anthu owerengeka komanso za anthu a cipiringu ca anthu (mwacitsanzo Cibvumbulutso 7.9). Ici citanthauza kuti pa mpando wa Mulungu padzakhala anthu ambiri kuti sakhoza kuwerengeka. Cifukwa cace sitikhoza kunena kuti iwo okhala pafupi ndi Mulungu ku Mwamba ndiwo anthu 144.000 cabe ndiponso sitikhoza kunena kuti ena onse adzakhala pa dziko lapansi.*

- Funsani aphunzi kuti moyo wosatha ndiwo ciani kulingana ndi iwo.
  Yankho:
  - Kudziwa Mulungu (Yohane 17.3). Ngati tidziwa Mulungu mwa Yesu amene ali Moyo (Yohane 14.6) tikhala ndi moyo wosatha. Ndiye moyo wosatha uyamba m'moyo uno!
  - Kukhala moyo moyenerera pamodzi ndi Mulungu Kumwamba.
- Fotokozani kuti umoyo wamuyaya ndi cotheka cifukwa ca Yesu cabe. Pamene Adamu ndi Hava anacimwa iwo anayenera imfa ndipo m'badwo wao wonse uyenera imfa (ici citanthauza kusiyanitsidwa ndi Mulungu muyayaya). Pamene Yesu anadza, Iye anakonza zimene ife tidataya. Cifukwa ca Iye tikhoza kukhala ndi moyo wosatha. Iye ndiye moyo (Yohane 14.6).
- Uzani aphunzi kuti Mulungu anabvumbulutsira Yohane zimene zidzacitika m'tsogolo Yesu atabweranso. Werengani pamodzi Cibvumbulutso 21.1-8 ndipo yankhani pamodzi mafunso awa:
  1. **Fotokozani mwacidule zimene Yohane anaona.**
     Yankho: Anaona zonse zokonzedwa ndi Mulungu: kumwamba ndi dziko lapansi. Anaona Ufumu wa Mulungu wokhazikidwa ndipo anamva Mulungu kulankhula.

  2. **Kodi moyo wosatha udzakhala wotani kulingana ndi ndime za 3 ndi 4?**
     Yankho: Ubwenzi wabwino pakati pa Mulungu ndi anthu ake, umoyo udzakhala bwino (kopanda matenda, imfa ndi zina zotere). Kumwamba ndi malo abwino koposa monga tingayerekeze.
  3. **Kodi ndani amene ali Woyamba ndi Wotsiriza monga mwa ndime ya 6?**
     Yankho: Mulungu/Yesu. Mulungu ndi wamuyaya. Ciyambi ca zonse ndi Wofikira.
  4. **Kodi Mulungu akamba ciani kuli iwo amene sanalape macimo ao?**
     Yankho: Adzakhala ku Gehena muyaya. Ici cichedwa imfa yaciwiri (matupi ao anafa kale, tsono mizimu yao idzazunzika nthawi zonse).
  5. **Kodi imfa yosatha ndi yotani?**
     Yankho: Iri yoipa kuposa imene tingayerekeze: kuzunzika m'moto ndi sulfure, kukhala ndi Satana muyaya.
  6. **Kodi mudzakhala kuti muyayaya?**
     Yankho: Aliyense ayankhe pa yekha.

- Tsirizani kuwerenga Baibulo ndi kuwawerengera Yohane 3.36 ndipo yesetsani kuwafulumizitsa kupeza cipulumutso ndi mtendere ndi Mulungu mwa Yesu Kristu.

## 4. Amen (5 minutes)

- Funsani aphunzi citanthauzo ca liu 'amen'. Kodi tiligwiritsa nchito pa kucita ciani?
- Fotokozani kuti liu 'amen' ndi liu m'Cihebri (Cihebri ndi cilankhulo ciyambi ca Baibulo) ndipo litanthauza: mosakayika ndi zoona. Litanthauza kuti cikhulupiriro cathu cobvomerezeka ndico cosakayika (kopanda kukaika) ndi coona (kulingana ndi Baibulo).
- Auzeni kukhala ocenjera pa kugwiritsa nchito liu 'amen': osalikamba kopanda kuganizirako koma cabe kutsimikizira cinthu cosakayika ndi coona.

## 5. Mayeso, osakakamiza (30 minutes)

- Lolani aphunzi kulemba mayeso.
- Congani mayeso. Mayankho abwino ali conco:

| | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| 1 B | 3 A | 5 B | 7 C | 9 C | 11 A | 13 A | 15 A | 17 B | 19 C |
| 2 A | 4 C | 6 C | 8 A | 10 B | 12 A | 14 B | 16 C | 18 C | 20 A |

## 6. Kutsiriza (5 minutes)

- Fotokozani mwacidule zimene zaphunzitsidwa lero ndipo kambani pamodzi: *I believe in God the Father, Almighty, Ndikhulupirira Mulungu Atate wamphamvu wa mphamvu zonse, wakulenga za kumwamba ndi za pansi. Ndikhulupirira Yesu Kristu, Mwana wake wobadwa yekha, Ambuye wathu amene anapatsidwa ndi Mzimu Woyera, nabadwa mwa Mariya namwaliyo, nasautsidwa kwa Pontio Pilato, namwalira, naikidwa m'manda. Natsikira kwa akufa. Tsiku lacitatu anaukanso kwa akufa nakwera Kumwamba, nakhala padzanja lamanja la Mulungu Atate wa mphamvu zonse, kucokera komweko adzadza kudzaweruza anthu amoyo ndi akufa. Ndikhulupirira Mzimu Woyera. Ndikhulupirira Mpingo wopatulika wa Kristu wa kwa anthu onse, ciyanjano ca oyera mtima, kukhululukidwa kwa macimo, kuukanso kwa thupi ndi moyo wosatha. Amen.*
- Yesetsani kuwafulumizitsa kusasewera ndi zimene akhulupirira ndiponso kuwerenga Baibulo!
- Pempherani.

## Mayeso *Cikhulupiriro*

Dzina: ………………………………………………………………..

1. Kodi titanthauzanji pa kunena 'Ndikhulupirira'?
   A. Tidziwa kuti Mulungu aliko ndiponso kuti akhala Kumwamba.
   B. Tikhala odzindikira kuti Baibulo ndi coonadi ndiponso kuti Yesu anakhululukira macimo athu.
   C. Sondo lirilonse timapita ku calichi ndipo tipereka copereka.

2. Ndi ciani cimene ciri coona kuli Mulungu?
   A. Mulungu ndi wamuyaya, Atatu, woyera ndi wacisomo.
   B. Mulungu Atate anafa pa mtanda.
   C. Mzimu Woyera si Mulungu.

3. Kodi dzina la Yesu litanthauza ciani?
   A. Mpulumutsi.
   B. Mbuye.
   C. Mphunzitsi.

4. Kodi dzina la Kristu litanthauza ciani?
   A. Mbusa.
   B. Mpulumutsi.
   C. Wodzodzedwa (wosankhidwa ndi kukonzedwa ndi Mulungu).

5. Kutanthauzanji kuti Yesu ndi Ambuye wathu?
   A. Tidziwa zonse za Iye.
   B. Ife ndife ake ndipo tifunikira kumumvera.
   C. Iye ndi wamuyaya.

6. Ndi ciani cimene ciri bodza?
   A. Yesu ali munthu weniweni ndi Mulungu weniweni.
   B. Mzimu Woyera anakonzera thupi kuti Yesu akabadwe.
   C. Atate wa Yesu ndi Yosefe.

7. M'Agalatiya 3.13 tiwerenga, 'Kristu anatiombola ku temberero la cilamulo, atakhala temberero m'malo mwathu; pakuti kwalembedwa, Wotembereredwa ali yense wopacikidwa pamtengo'. Kodi temberero la cilamulo ndilo ciani?
   A. Temberero la cilamulo litanthauza kuti kudula mitengo ndi koipa.
   B. Temberero la cilamulo litanthauza kuti malamulo ndi oipa.
   C. Temberero la cilamulo ndilo temberero la anthu locokera kwa Mulungu cifukwa ca kusamvera malamulo ake.

8. Cifukwa ciani Yesu anati, 'Kwatha'?
   A. Pakuti Iye anatha zonse zimene adayenera kucita kupulumutsa anthu ake ku macimo ao.
   B. Pakuti Iye anatopa.
   C. Pakuti adani ake anamupambana mwa kumupha.

9. Kodi Yesu anauka kwa akufa patapita masiku angati?
   A. Patapita masiku atatu (3).
   B. Patapita masiku anai (4).
   C. Patapita masiku asanu (5).

10. Kodi Yesu ali kucita ciani m'Mwamba?
   A. Apumula ndi kuyembekezera nthawi ya kubweranso kwake.
   B. Alamulira, atuma Mzimu wake Woyera ndipo apempherera anthu ake.
   C. Aimbira ulemerero wa Mulungu.

11. Cabodza ndi citi pokhuza Mzimu Woyera?
    A. Kopanda Mzimu Woyera tikhoza kufika Kumwamba.
    B. Aphunzitsa anthu ocimwa kulapa ndi kudalira pa Yesu kuti apulumuke.
    C. Akhala mwa anthu a Mulungu.

12. Kodi caka ciriconse timakumbukira ciani pa tsiku la Pentekoste?
    A. Kutumidwa kwa Mzimu Woyera.
    B. Kuuka kwa akufa kwa Yesu.
    C. Kubwerera Kumwamba kwa Yesu.

13. Cifukwa ciani tikamba kuti mpingo wa Mulungu ndiwo 'wopatulika' ndi 'wa kwa anthu onse'?
    A. Pakuti mpingo wa Mulungu ndi wa anthu onse a Mulungu a pa dziko lonse lapansi.
    B. Pakuti anthu a Mulungu amakomana pa malo apadera kuti ampembedze.
    C. Pakuti anthu onse ali m'banja la Mulungu.

14. Kodi tiulula ciani pamene tinena 'ciyanjano ca oyera mtima'?
    A. Tiulula kuti anthu a Mulungu a Kumwamba ayanjana.
    B. Tiulula kuti anthu onse a Mulungu ali m'ubwenzi wapadera ndi Mulungu ndi wina ndi mnzace.
    C. Tiulula kuti anthu a Mulungu amatenga mbali m'Mgonero wa Ambuye

15. Ndi ciani cimene cicitika pamene Yesu akhululukira macimo athu?
    A. Ndife opanda mlandu m'malo mwa olakwa, ndife odalitsika m'malo mwa otembereredwa, ndife okhala pafupi ndi Mulungu m'malo mwa kukhala kutali ndi Iye.
    B. Tidzapita Kumwamba mosacedwa.
    C. Sitidzacimwanso.

16. Kodi ndi liti pamene matupi athu adzaukanso kwa akufa?
    A. Sitidziwa.
    B. Matupi athu sadzaukanso.
    C. Pamene Yesu adzabweranso ku dziko lapansi.

17. Kodi moyo wosatha ndiwo ciani?
    A. Kukhala okondwera m'ciriconse cimene cicitika m'umoyo wathu.
    B. Kudziwa Mulungu mwa Yesu Kristu ndi kukhala naye Kumwamba.
    C. Kukhala ndi moyo nthawi yaitali monga mwa cifuniro cathu.

18. Kodi ndani amene ali ndi moyo wosatha?
    A. Aliyense amene anacita zabwino zotheka m'moyo wake.
    B. Sitidziwa mpaka titamwalira.
    C. Aliyense wokhulupirira Yesu yekha kukhala Mpulumutsi wake ku macimo ake.

19. Kodi anthu a Mulungu ndi ayani?
    A. Azibusa ndi aneneri.
    B. Anthu amene adziwa kulankhula malilime ndi kucita zodabwitsa.
    C. Aliyense amene analandira Yesu kukhala Mpulumutsi wake mwa cisomo.

20. Kodi kuli mpata kuti tingafike Kumwamba mwa mphamvu yathu?
    A. Iai, tiyenera kulapa macimo athu ndi kupempha Mulungu cikhululukiro mwa Yesu.
    B. Inde, ngati timayesa kucita nchito zabwino zoposa m'moyo wathu.
    C. Inde, ngati timamvera abusa ndi makolo athu.

# Zikomo!